

# MABWANA, IFE TIKUFUNA TIMUWONE YESU

🦋 (...?...Ine ndinayesetsa kukuyimbirani inu masana ano, mwamphamvu momwe ine ndikanathera, inu simunali kunyumba pamene ine ndimayesetsa kuyimba. Heyi, ngati muli ndi uthenga mupitirire ndipo ine ndingodikirira. Inu mukutsimikiza, tsopano? Inu mulibe kanthu koti mulalikire...?...)

[M'bale Neville akuti, “Ndife okondwa kwambiri usikuuno, M'bale Branham amangondifunsa ine ngati ndinali ndi uthenga, iye sanandipeze ine, koma iye samayenera kuti andipeze ine. Amen. Ndine wokondwa, usikuuno, pakuti ine ndinati ndinachiyesa icho chapamwamba kwambiri kuti iye ali pano ngakhalebe. Ndipo ndakondowezeka, mochuluka kuposa chirichonse chimene ine ndiri nacho pa Khristimasi, kudziwa kuti iye ali pano. Ndipo chotero Ambuye amudalitse iye pamene iye akubwera usikuuno. Ngati iye angoyima pano, izo zingakhale zabwino. Mulungu alemenzeke! Koma ndine wokondwa kuti iye ali pano, ndipo Ambuye amudalitse iye pamene akhale akubwera.”—Mkonzi].

Zikomo inu, M'bale Neville. Zikomo.

<sup>2</sup> Madzulo abwino, abwenzi. Ine ndimanena kwa M'bale Neville, ine—ine ndinayesetsa kumuyimbira iye kunyumba yake masana ano. Ine ndinanena kwa anthu ochokera uko ku Georgia, ndi kozungulira, sabata yathayi, kuti ine sindimaganiza kuti ine ndikanakhala pano lero, chifukwa anthu ambiri amabwera.

<sup>3</sup> Ndipo, komabe, pa Khristimasi, inu mukudziwa, ana aang'ono, inu simungawauze iwo mosiyana. Iwo, basi, ndi nthawi ya Khristimasi kwa iwo. Ndipo iwo sangati apachike masokosi awo aang'ono, pangakhale kuti pali chinachake. Ndi cha mwambo, ngakhale mu fuko lathu, kuti iwo angapachike sokosi, ndi chinachake chimzake. Bwanji, ine ndinkatero, pamene ndinali mwana, ndipo—ndipo ngakhale monga—zotalikirana ndi Lemba, njira yozolowereka momwe izo zimakhallira. Komabe, ana ali, iwo amawamva ana ena akuti, “Chabwino, ine ndiri ndi *ichi* cha pa Khristimasi. Ine ndiri nacho *ichi*.” Ana aang'onowo amayima pozungulira, amayang'ana, inu mukudziwa. Inu, inu simungawapangitse iwo kumvetse. Mukuona? Koteri, basi, Khristimasi ili pano kuti idzakhale. Eya.

<sup>4</sup> Ndipo ilo si tsiku lobadwa la Ambuye wathu, nthawi imene Iye anabadwa. Tsopano, ngati mungapite pa yanu...pa mapu a dziko lapansi, ndi kuyang'ana, Yudeya ali pafupifupi pansa pa

equator monga ili liri pamwamba pake. Kotero ife tikupeza kuti, mu Yudeya, mmapiri amenewo kumtunda uko, kuti kuli chisanu. Mai! Kuli chisanu chochuluka kuposa chimene chiripo kuno. Kotero azibusa sakanakhoza kukhala pa . . . pa phiri pa nthawi imeneyo, akuweta nkhoa zawo.

<sup>5</sup> Ndipo chinthu china, Iye, izo zingakhale zotsutsana ndi chirengedwe chonse. Mukuona? Ana ankhoa ndi zina zotero zimabadwa mu nyengo yamasika, osati nthawi ino ya chaka. Ana a nkhoa samabadwa nthawi ino. A—nkhoa zazikazi sizimabereka nthawi ino. Ndipo Iye anali Mwanawankhoa wa Mulungu, mwaona. Kotero kumeneko, Iye anabadwa cha mu, iwo amati, cha mu Epulo nthawi inayake, pakati pa mwezi wa Epulo, chinachake monga chomwecho.

<sup>6</sup> Koma, ili pokhala 25 ya Disembala, bwanji, kulipanga ilo kukhala tsiku lobadwa. Ili ndi tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa. Mukuona? Baala wa Chiroma, mulungu wa dzuwa. Mukuona? Ndipo dzuwa liri ndendende basi mwatheka panthawi ino. Ndipo kuyambira pa 20 mpaka pa 25 inali nthawi imene chikondwerero cha Chiroma chinkachitika, pokondwerera tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa. Ndipo chotero iwo anati, “Chabwino, tsopano, kuti tiwakondweretse awiri onse Mkristu ndi wachikunja, ife tipanga, mmalo mwa mulungu wa dzuwa, Mwana wa Mulungu ndi mulungu wa dzuwa, limodzi. Kotero ife tiziyika izo zonse pamodzi ndi kulipanga ilo kukhala tsiku lobadwa lomwelo, ndi kulipanga ilo kukhala pa 25.” Kotero izo zinkawoneka kuti zinakondweretsa achikunja ndi mpingo wamba mu nthawi imeneyo, mu mpingo woyamba wa Roma. Zinali chabe. . . Izo zinali zabwino basi ndi iwo, kotero iwo sankasamala. Kotero iwo anazipanga izo kukhala zonse ziwiri tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa ndi la Mwana wa Mulungu.

<sup>7</sup> Tsopano, tsiku lalitali kwambiri mu chaka ndi pafupifupi la 21 kapena la 22, usiku wautali kwambiri, ine ndikutanthauza, mu chaka, ndi pafupifupi wa pa 21 kapena wa pa 22, pamene, mu dongosolo la dzuwa, dzuwa limakhala likungonjanja, kubwereranso. Tsopano iwo amayamba kukhala ndi mphindi kapena maminiti pang’ono chabe kutalikirapo. Ndiyeno nthawiyina mu Juni kapena Julaye, ife timakhala ndi tsiku lalitali kwambiri mu chaka.

Kotero, koma, Khrisimasi ili kuno kuti idzakhale, kotero ife—ife sitingaziletse izo.

<sup>8</sup> Matayala opanda machubu ali kuno kuti adzakhale. Ndimadana nawo, koma iwo ali—iwo ali kuno kuti adzakhale. Uh-huh. Uko nkulondola.

<sup>9</sup> Akazi osavala, ali kuno kuti adzakhale. Akabudula, iwo akhala. Ndizo zonse. Iwo azifupikirabe nthawi zonse, kotero palibe chirichonse chimene ndingachite pa zimenezo.

Ine ndimangonena kuti izo ndi zolakwika. Muzikhala ndi Iwo, ndipo uko nkulondola.

<sup>10</sup> Tchimo, ilo liri kuno kuti lidzakhale. Liri kuno kuti lidzakhale. Ife tizikhala nalo ilo, mopitirira ndi mopitirira. Chotero, basi, ilo liri kuno kuti lidzakhale mpakana Yesu adzabwere. Ndipo zinthu zonsezi ziri kuno kuti zidzakhale. Tsopano, ine sindimakhulupirira . . .

<sup>11</sup> Ndiroleni ine ndifotokoze izi momveka bwino. Ine sindimakhulupirira kuti Yesu akanamasamala za tsiku limene inu mukanati muzipembedza tsiku Lake lobadwa, ngati ilo liri pa 25, pa 26, kapena kaya ndi Epulo, Meyi, Juni, Julaye, kapena nthawi iliyonse imene iyo ingakhale, basi yoti inu muzipembedza, inu muzimupembedza Iye pa tsiku lirilonse.

<sup>12</sup> Koma apa pali chimene icho chiri. Iwo anachotsa kupatulikako kuchokera ku Khristimasi, nkuzipanga izo osati Khristimasi koma, tsiku lopembedza, koma chikondwerero. Mukuona? Ife siti. . . Inu mumawamva anthu akuti, “Ife tikukakondwerera Khristimasi.” Uko nkulakwitsa. Ife sitikuyenera konse kumakondwerera Khristimasi. Khristimasi ndi tsiku lopembedza, osati chikondwerero.

<sup>13</sup> Ife timakondwerera tsiku lobadwa la Lincoln. Ife timakondwerera tsiku lobadwa la Washington. Ngati inu mukanakhala Kummwera kwakuya, ife tikanamakondwerera tsiku lobadwa la Lee, kapena—kapena Jackson. Tsiku lobadwa lawo ndi chikondwerero.

<sup>14</sup> Koma tsiku lobadwa la Khristu, ine ndikukhulupirira, likuyenera kukhala tsiku la kudzipatula, kupembedza, mmalo mwa usikuuno. Za anthu ku tchalitchi, ali pa mawondo awo, akupemphera, kumuthokoza Mulungu chifukwa cha Mphatso ya Khristimasi yeniyeni.

<sup>15</sup> Nsapato zazitali zidendene, ndi nkhope zopenta, ndi zikhotho zazitali kumbuyo, ndipo zikho za kachasu zimenyetsedwa, china ndi chimzake. Ndipo ma teni amasauzande kuchulukitsa masauzande ama dola a mowa, ndi ndudu, ndi fodya zigawidwa usikuuno. Pamene, masauzande a osauka, aang’ono, ana anjala akugona opanda chakudya kapena malo oti agonetsepo mutu wawo.

<sup>16</sup> Kupembedza, nchimene ife tikusowa. Chikondwerero ndi chimene ife tiri nacho. Oh, izo zonse ndi zabwino. Izo, izo siziri. . . siziri bwino, koma ife sitingathe kuziletsa izo. Izo ziri kuno kuti zidzakhale. Ife, ife tikhala ndi Khristimasi chimodzimodzi basi.

<sup>17</sup> Ndipo mawu akuti *Khristimasi*, Khristimasi anachokera ku mawu akuti “misa ya Khristu,” Misa ya Khristu, K-h-r-i-s-i-m-a-s-i. Mukuona? Misa ya Khristu, ndi mwambo wa Chikatolika.

<sup>18</sup> Ndipo wanga wamng'ono, mmodzi wa ana anga aakazi, ine sindingamutchule iye kuti mwana panonso, Becky, ankayenera kuti alembe nkhanu tsiku lina, ya nthano, zopeka. Ndipo ine ndinati, "Ungolemba za Santa Claus." Ndi—ndi zimenezo. Santa Claus watenga malo a Khristu. Ndipo Santa Claus, sipanakhalepo munthu woteroyi. Mukuona? Iwo mwamtheradi ndi mwambo wa Chikatolika, popanda chirichonse chochita ndi Achiprotetanti kapena chirichonse cha izo, mwaona, kapena Khristumasi, kapena kubadwa kwa Khristu, osati nkomwe. Koma Santa ali kuno kuti adzakhale.

<sup>19</sup> Koma tsiku lina Yesu adzabwera kuti adzakhale. Ndiye Mmodziyo amene ife tikumuyembekezera.

<sup>20</sup> Tsopano, ine ndithudi ndikanakonda M'bale Neville akanatenga guwa ili, usikuuno. Chifukwa, izo ziri, ine ndinawauza anthu kuti ndikhala kutali lero. Ndipo ngati ine ndikanabwera ndi kudzanena chirichonse, ine ndikanadzapanga tepi. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti iwo... Kodi inu muli ndi tepi rekoda ikujambula, mulinayo iyo? [M'bale Neville akuti, "Inde."—Mkonzi]. Kudzapanga tepi. Kutu ngati Mzimu Woyera mu nthawi ya msonkhano ungayankhule chirichonse, izo zikhosha kukhala kuti iwo akhosha, iwo akhosha kudzawumvetsera Iwo. Mukuona?

<sup>21</sup> Ine ndiri ndi Malemba ena, ndi zina zotero, ndalemba apa, mutu wawung'ono. Ndipo ine sindikudziwa; ine ndikudalira kuti Ambuye adalitsa izo. Koma chinthu chake ndi chakuti, kawirikawiri, pa mausiku a Lamlungu awa, anthu amakhala atachoka kuno pafupifupi naini, kapena maminiti teni pambuyo pake, ndipo zikhala bwino kuti muzituluka isanakwane wani.

<sup>22</sup> Kotero, koma ine ndikuganiza kuti pali wotchi. Uh-huh. [M'bale Neville akuti, "Uko nkulondola."—Mkonzi]. Chiyani? Chinachake, msonkhano wa pakati pa usiku? ["Ayi, osati usikuuno, kuno."] Ine ndikutanthauza... Ayi, osati usikuuno, ayi. Kutu, iye—iye amaganiza kuti mwinamwake ine ndinali ndita, nditazisokoneza, uwo ndi usiku wa Chaka Chatsopano.

<sup>23</sup> Chabwino, ife tikuyembekezera nthawi yopambana, usiku wa Chaka Chatsopano. Imeneyo ndi nthawi imene ife, aliyense, abale onse amabweramo, ndipo ife timakhala ndi chiyanjano chachikulu, wina ndi mzake, pa usiku wa Chaka Chatsopano.

<sup>24</sup> Tsopano, koma ine ndimangokusereulani inu za izo. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti izo sizinajambulidwe pa tepi.

<sup>25</sup> Titi, tsiku lina, tikupanga tepi, ine ndimagunda chinthu *ichi* pafupifupi nthawi zingapo, ndipo—ndipo ine ndinangoyiwononga tepiyo, pa *Chikhristu Kutsutsana Ndi Chikunja*. Matepiwo anawonongeka. Kotero ngati matepiwo a—akusewera kapena akubwera, ndikanakonda kuti aliyense amene akujambula iwo abwere pakhomopo. Mungotsegula chitsekochi kapena chinachake, chotero kuti ine ndidziwe kuti

iwo ayamba kujambulidwa tsopano. Ine ndiwona mbali imene chinthu *ichi* chatembenuzidwira, ngati icho chikugwira ntchito. Chabwino. Chabwino. Izo ziribwino. Ine ndichiphimba icho, ndipita kumbali inayi. Sindinazolowere zimenezo.

<sup>26</sup> Chabwino, ine ndikufuna kuti nditenge mwayi uwu kuti ndithokoze mpingo uno ndi mamembala ake, pa zinthu zabwino zimene inu munandipatsa ine pa Khristimasi. Kanthawi kapitako, mwana wanga anabwera ndipo anandipatsa ine bokosi lalikulu kwambiri. Ndipo ine ndinali mu... chipinda changa chowerengera, ndikuwerenga. Ine ndinatsegula ilo, ndipo ndinapeza suti yatsopano ya zovala yochokera ku kachisi kuno. Ndi zinthu zazing'ono zapadera zimene anthu anditumizira ine, basi kumtunda uko, zimene sindinazitsegule mpaka Joe atabwera usikuuno ndi kudzatsegula zakezo. Ndiyeno, ine—ine ndithudi ndikuyamikira zimenezo. Ambuye akudalitseni inu. Ine ndikanakonda ndikanapereka mphatso za Khristimasi kwa aliynse. Ine sindingathe kuchita zimenezo. Inu mukudziwa momwe zimakhallira. Iwe basi sungathe kuchita zimenezo. Ndizo zonse. Ngati iwe—ngati iwe ungapereke kwa mmodzi, izo zimawonetsera ulemu monga choncho. Iwe sungakhoze basi kuchita zimenezo. Mtumiki sangathe basi kuchita zimenezo.

<sup>27</sup> Ndipo ine ndamva kuti M'bale Neville, mmawa uno, anapatsidwa chikhotho chatsopano. Ndine woyamikira kwambiri kwa inu nonse, chifukwa cha m'bale wanga.

<sup>28</sup> Pali chinsinsi chaching'ono kwa zimenezo, chimene Billy Paul ndi ine timachidziwa. Inu mukudziwa, ndine wochedwa kwambiri pa chirichonse, ine...kuzindikira, mulimonse, za chirichonse. Billy amandiuza ine, tsiku lina. Iye anati, "Inu mukudziwa, adadi, ine ndinali uko ku sitolo yapamwamba. Ndipo," anati, "kodi ine ndinakomana ndi ndani kumeneko?" Iye amanjenjemera pang'ono poyankhula. "M'bale Neville, ndipo," anati, "iye anali atavala chikhotho, sichimawoneka bwino."

Ndipo ine ndinati, "Kodi changa chingamukwane iye?" Uhuh.

<sup>29</sup> Ndipo chotero, ndipo iye anati, "Ayi. Iye ndi munthu wamkulu kwambiri kuposa momwe inu muliri."

Kotero ine ndinati, "Oh, ine ndingopita uko basi kuti ndikamupezere iye chimodzi."

<sup>30</sup> Kotero, ndiye ndinadzatenga cheke changa kuchokera ku tchalitchi kuno, monga iye amachitira. Kotero pa nthawi imeneyo, Billy anabwera akuthamanga ali ndi mawu aakulu achikoka, ndipo akumwetulira pa nkhoze yake, "Adadi, mpingo ukamupezera iye chimodzi." Chabwino, ine ndikudziwa kuti mpingo ndithudi ukhoza kumupezera iye chabwinoko pang'ono kuposa changa, kotero ine ndinaganiza, "Izo ndi zopambana basi, kotero ife tonse tikhoza kukhala nazo." Koma ife tikudziwa

kuti icho chinabwera pa malo abwino kwenikweni, pamene M'bale Neville amasowa chikhotho chimenecho.

<sup>31</sup> Inu mukudziwa, ine ndikufuna ndikuuzeni inu chinachake chaching'ono chokhudza izo. Ine ndimawerenga mu mbiriyakale. Ndizo zonse zimene ine ndimapanga m'masabata angapo apitawa, miyezi kapena awiri, zakhala ziri kuwerenga mbiriyakale ya Baibulo. Ine nthawiyina ndinawerengapo a . . .

<sup>32</sup> Bukhu langa loyamba linali Chipangano Chakale, chimene Mulungu anali mu Chipangano Chakale. Kenako ndinadzawerenga Chipangano Chatsopano, ndi kuwona chimene Mulungu anali, kuti ndifanizitse izo lero, chifukwa ine ndikudziwa kuti Iye akuyenera kukhalabe yemweyo. Mukuona?

<sup>33</sup> Ndiye pali malo amodzi a mpingo amene ine ndinawaphonya, iwo anali pakati pa nthawi ya kupita kwa mtumwi wotsiriza mpaka kudza kwa m'badwo wa mdima, pamene mpingo wa Katolika unadzakhala mu ulamuliro. Iwo anataya zozizwitsa zonse, ndi Zauzimu zonse, zinachoka mu tchalitchi, chirichonse. Ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndidziwe chimene chinachitika mu nthawi imeneyo, kotero ine ndangotengapo zina za mbirizakale zamakedzana kwambiri zomwe ziripo, monga *Two Babylons* la Hislop, ndi *Pilgrim Church* la Broadbent, *Foxes Book Of The Martyrs*, *The Post-Nicene Fathers*, *Nicene Council*, *Pre-Nicene Council*, ndi azambiriyakale opambana onsewo amene analembe mu nthawi zimenezo, moyo wa amuna onse ofunikira amenewo. Pamene ine ndimawerenga iwo, izo zimawoneka ngati ine ndimakhoza kumva *Salmo La Moyo* la Longfellow:

Miyoyo ya amuna aakulu yonse imatikumbutsa  
ife

Tikhoza kupanga miyoyo yathu kukhala  
yapamwamba,

Ndi kulekana, kusiya kumbuyo kwathu

Mphondero pa mchenga wa nthawi.

<sup>34</sup> Pamene ine ndinawona zimene amuna ndi akazi amenewo anadutsamo, kumbuyo uko, ndi kuwona, kuti awusunge Uthenga womwewu! Ndipo pamene iwo ank'alalikira Uthenga womwewu, chinthu chomwecho chimene chinkachitika mu Chipangano Chakale, Chipangano Chatsopano, ndipo nthawi imeneyonso chimodzimodzi basi. Kotero izo zimapereka kwa Iwo imodzi, ziwiri, mboni zitatu. Mawu aliwonse amakhazikitsidwa. Mulungu yemweyo amene ankachita ndi aneneri akale, ankachita ndi atumwi, ndipo ankachita ndi abale a pre-Nicene.

<sup>35</sup> Ndipo pano Iye ali lero, akuchita mwanjira yomweyo ndi anthu Ake, ndi zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, Uthenga womwewo, mphamvu yomweyo, Mulungu yemweyo, chirichonse. Ndi zitatu ngati mboni, kwa ife, kuti *Ichì* ndi

Choonadi. *Ichi* ndi Choonadi. Mulungu anachipereka icho mu zipangano zitatu. Mukuona? Mbiriyakale imeneyo ndi...

<sup>36</sup> Baibulo ndi mbiriyakale ya chimene Mulungu anali, chimodzimodzi mbiriyakale ya Chipangano Chakale.

<sup>37</sup> Chipangano Chatsopano ndi mbiriyakale ya—ya Chipangano Chatsopano.

<sup>38</sup> Ndipo *Nicene Council And Fathers*, ndi *Post-Nicene Council*, ndi mbiriyakale ya mpingo ya nthawi imeneyo.

<sup>39</sup> Ndipo tsopano mbiriyakale ikupangidwanso basi monga iyo inkachitira. Imene, mbiriyakale iyi siyidzalembedwa konse. Ayi. Ziri pafupi kwambiri ndi Kudzako tsopano.

<sup>40</sup> Ndipo Mulungu amuthandize munthu mmasiku ano, anthu amene amayesetsa kufunafuna ulemu wa anthu, amuna amene amayesetsa ku—kudzipanga okha kukhala otchuka, kapena pakati pa anthu. Kodi inu simukudziwa, kuti munthu ameneyo, pamene iye afa, zonsezo zimafa limodzi ndi iye? “Koma funani kuti mupeze chuma cha Kumwamba. Icho sichidzatha konse.”

<sup>41</sup> Madalitso olemera kwambiri a Mulungu akhale pa inu nonse. Ine ndinawauza iwo, usikuuno, kawirikawiri umakhala mwambo wanga kuti ndipite ku tchalitchi kwinakwake Lamlungu, ngati ine ndingakhoze kutero.

<sup>42</sup> Ine, lero, mmawa uno, ine ndimafuna kuti ndibwere kuno moyipa kwenikweni, ndi kudzamva uthenga wa M'bale Neville. Koma nditatha kupanga lonjezo limenelo, ndiye ine sindimafuna kuti ndiliswe ilo.

<sup>43</sup> Kotero ndiye ine ndimayesera kuti ndimvetsere ku mawailesi, ndi—ndi zina zotero, ndipo zonse zimene ine ndimakhoza kuzimva zinali, “Mwamsanga ukatha msonkhano uno, ife tonse tikakomana mu chipinda cha nkhomaliro ndipo tikakhala ndi khofi limodzi. Ndipo ife tika...” Kodi mpingo wafika ku chiyani? Ndi loji. Bwanji osangonena kuti “loji” mmalo mwa tchalitchi. Tchalitchi sichimayenera kuti chizichita zimenezo. Tchalitchi si msonkhano wa khofi, kapena nkhomaliro, kapena zakudya za madzulo, ndi zinthu monga chomwecho.

<sup>44</sup> Ife timakhala ndi mgonero ndi Ambuye. Tchalitchi, uko ndi kumene ife timayanjana ndi Iye.

<sup>45</sup> Ine ndinati kwa mkazi wanga, “Wokondedwa, ine—ine ndikukhala wotsutsa kwambiri, ine ndikudana nazo kuti ndipite kumusi ku kachisi, kapena kulowa pa guwa.” Oh, pamene ndikukalamba, zikuwoneka ngati, ndikumalipirayipirabe. Ndipo ine—ine—ine sindi—ine sindikufuna kuti ndizikhala chomwecho, monga choncho. Koma muli Chinachake mkati mwanga chimene chikundikankha ine, kuti ndikhale monga chomwecho.

<sup>46</sup> Ndiye ine ndinati, “Kodi ine ndikusokonezeka mmalingaliro anga? Nchifukwa chiyani ine sindikupita ndi gulu lina lonselo?

Bwanji ine osamapita monga abale enawo? Nchifukwa chiyani sindikutha kudziphezera bungwe, kumanga mozungulira ilo momwe iwo amachitira? Kapena, bwanji ine osapita kunja uko ndi kusiya kumawakhoma anthu ndi zinthu monga chomwecho? Nchifukwa chiyani sindikumachita zimenezo?” Ine ndinati ndiye, ine ndikuganiza, “Kodi ine ndasokonezeka mmalingaliro anga?”

<sup>47</sup> Kenako ndinadzabwerera ku Mawu, ndipo izo zinali pamenepo. Ine ndikuyenera kukhala ndi Mawu amenewo.

<sup>48</sup> Ine ndinati, “Ine, ngati izo zikanapanda kukhala chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndipo ine nkumadziwa kuti Mulungu analipo, ine ndikanakhoza kudzimangira ndekha kanyumba kakang’ono kwina kwake, kutali kwambiri mmbuyo ku British Columbia, kutali komwe uko mu Canada, mmapiri kumene ine sindikanamakhoza kumuwona munthu, kamodzi pa chaka. Ndipo kumeneko ine ndikanamakhoza kumamva Liwu la Mulungu mmitsinje yamafunde, ndi kumamumva Iye pamene Iye akufuula mokweza, mu nkhandwe pamwamba pa phiri. Ine ndikanamakhoza kumamumva Iye pamene Iye akunong’ona kupyolera mmitengo yayikulu ya paini, ndi kumayang’ana pa nkhope Yake yokondeka mu galasi la nyanja, pamene iyo ikunyezimiritsa mapiri aakulu a chisanu. Bwanji, ine ndikanamamupembedza Mulungu tsiku lililonse la moyo wanga, kumbuyo uko. Ine ndikudziwa kuti ndikanakhala weniweni kwambiri pa za Mulungu, kumbuyo uko, kuposa momwe ine ndingakhaliye pomvetsera ku migonero ya khofi ndi maphwando a tiyi, ndi mitundu yonse iyi ya zinthu izi zimene ife tiri nazo lero, zotchedwa tchalitchi; tizikhulupiriro, ndi zopeka, ndi nthano, ndi china chirichonse, kuti zitenge malo a Uthenga.”

<sup>49</sup> Ine kulibwino ndiwerenge Lemba lina, sichoncho ine, ndi kuyambapo. Tsopano, ife tisanawerenge, tiyeni tiyankhule kwa Iye Amene analemba Iwo, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

<sup>50</sup> Nonse amene muli ndi chopempha usikuuno, uwu pokhala usiku wa Khrisimasi, mukhoza kukhala ndi chinachake chonga ichi, “O Ambuye, ndine woyamikira mu mtima mwanga chifukwa cha Khristu, ndipo ine ndikufuna kuti ndibwere moyandikira pang’ono chabe tsopano kuposa kale. Ine ndikufuna kuti ndisabwerere kodyera ng’ombe ku khola, koma ine ndikufuna kuti ndiwupange mtima wanga kukhala modyera ng’ombe, osati kwa Khristu khanda, koma Khristu amene ali Mulungu, Emanuele.” Kodi inu mungalole izo zidziwike ndi dzanja lanu lokwezedwa kwa Khristu? Ambuye apereke chopempha chanu.

<sup>51</sup> Atate Akumwamba, tsopano ife tasonkhana mnyumba imene imatchedwa nyumba ya pemphero, malo amene ife timabwera pamodzi kudzapembedza Ambuye Yesu mu ntchito Zake zonse zazikulu, ndi kudzaphunzitsa Mawu Ake, ndi kukhulupirira kuti

Iye ndi Mawu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha usiku uno, ndi mimwayi yake imene ili patsogolo pathu, kuti tibweretse Mawu a Mulungu wamoyo kwa anthu amoyo, ndipo makamaka kwa iwo amene akukhala moyo mwa Khristu Yesu, amene akonzedwanso, abadwa mwatsopano, asanduka zolengedwa zatsopano. Ndi mwayi umene ife tiri nawo kuti tipereke—zoona kwa iwo amene si zolengedwa zatsopano mwa Khristu, kuti, usiku uno, iwo akhoze kukhala zolengedwa zatsopano mwa Khristu. Perekani kwa aliyense wa anthu awa chokhumba cha mtima wawo.

<sup>52</sup> Ndipo mulole kuti iwo, usikuuno, ngati iwo sanateropo, abwere mu wawukulu wa dziko lonse uwu, Mpingo wa katolika; uwu, *katolika*, monga iwo uliri mu “dziko lonse,” wautumwi, oyera obadwa mwatsopano a Mulungu wamoyo. Perekani izi, Ambuye. Mulole kuti munthu aliyense akhale membala wa Iwo. Chifukwa, Ilo ndi Thupi, osati nyumba, koma Thupi, Thupi la Khristu, ndipo ndife ziwalo za Thupi ili. Perekani izi, Ambuye.

<sup>53</sup> Mulole kuti mphatso zazikulu zochokera kwa Khristu zitsanuliridwe pa anthu, usikuuno, zomwe ziri mu Thupilo. Osati phukusi losindikizidwa, osati liri ndi mphatso za Khristimasi mmenemo, monga momwe ife anthu apadziko lapansi timaperekera kwa wina ndi mzake, poyamikira chikondi chathu kwa wina ndi mzake. Koma mulole kuti icho chikhale chisindikizo cha Mzimu Woyera chikubwera pansu mu moyo wa mtundu wa anthu, kuwapatsa iwo Moyo wachisavundi. Adalitseni iwo onse, pamodzi, Atate.

<sup>54</sup> Pamene, usikuuno, monga momwe ife tikudziwira, pokhala athanzi ndi okondwa, moto wabwino wotentha utakhala pafupi, denga pa mutu wathu, ndipo nkumaganiza za masauzande kuzungulira dziko lapansi, opanda malo opitako. Atate Akumwamba, mutichitire ife chifundo, ndipo mupereke chopempha ichi.

<sup>55</sup> Ife tikupempha usikuuno kuti Inu mudalitse Mawu pamene Iwo azipita tsopano.

<sup>56</sup> Mudalitse abusa athu. Mudalitse matrasti ndi madikoni a mpingo, ndi aliyense amene amayanjana ndi iwo, mu umembala wa Thupili, pokhala obadwa mwatsopano. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>57</sup> Monga ine ndinayambira, mphindi zingapo zapitazo, kuti ndinene, mu kuwerenga kwa oyera. Martin Woyera anabwera usiku wina wozizira, ndipo iye anamupeza munthu wachikulire wosauka atagona, atazizidwa, pa chipata. Ndipo iye anawawona anthu akudutsa, amene anali okhoza kumupatsa bambo wokalambayo a—chikhotho cha mtundu winawake, koma iwo sanachite zimenezo. Ndipo iye podziwa ndiye kuti inali ntchito yake kuti achite zimenezo, komabe abambo ake ndi amayi onse anali achikunja. Koma iye anali msirikali, kotero iye anavula

chikhotho chake, anatenga lupanga lake ndipo anachidula icho, mwatheka, pawiri, ndipo anamukulunga munthu wokalambayo mmenemo, ndipo kenako anapitirira. Ndipo anthu anamuseka iye, anamunyoza iye. Anati, “Msirikali wowoneka-moseketsa! Wotentheka bwanji!”

<sup>58</sup> Koma usiku wotsatirawo, iye anadzutsidwa, kumalo kokhala asirikali kumene iye ankakhalako, ndipo iye anali mmasomphenya. Ndipo anayang’ana, ndipo iye anali mchipinda, ndipo apo panayima Yesu ndi gulu la Angelo atayima momuzungulira Iye. Ndipo Yesu anali ndi chidutswa cha mkanjo ichi chitakulungidwa pa Iye, chikhotho. Ndipo Iye anati kwa Angelowo, “Kodi inu mukudziwa kumene Ine ndinachitenga ichi?”

Ndipo iwo anati, “Ayi, Ambuye wanga.”

Iye anati, “Martin anadzandikulunga Ine mu ichi.”

<sup>59</sup> Kotero M’bale Martin anadziwa, pamenepo, kuti uko kunali kuyitana kwake kwa utumiki. Chifukwa, pamene anamukulunga bambo wokalamba uja mu mkanjo umenewo, Yesu anali mwa bambo wachikulire ameneyo. Kotero ngati Iye anali mwa bambo wachikulireyo, monga ife tingamutchulire kuti wopemphetsa kapena wopanda kwawo, atagona pa msewu, Yesu adzabwera kwa aliyense wa ife. Ndiye iye anadziwa kuti, “Chimene inu mwachita kwa aang’ono a awa, aang’ono Anga, inu mwachita icho kwa Ine.” Mulungu atithandize ife kuti tizikumbukira zimenezo.

<sup>60</sup> Tsopano, inu amene muli ndi Mabaibulo anu ndipo mukufuna kuti mulembe mutuwo, Ine ndikufuna kuti ndiwerenge malo awiri kuchokera mu Zolemba Zoyera usikuuno, amodzi ochokera mu Yesaya, ndipo enawo ochokera mu Yohane Woyera. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Yesaya, mutu wa 42; ndi kuchokera ku Yohane Woyera, mutu wa 12. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge Malembawo. Yesaya 42 kuyambira ndi 1, ndime ya 1, ndipo kupita mmusi kuphatikizira ndime ya 7.

*Taonani wantchito wanga, amene ine ndikumuthandizira; wosankhidwa wanga, mwa yemwe moyo wanga ukondwera; ine ndayika mzimu wanga pa iye: iye adzabweretsa chiweruzo kwa Amitundu.*

*Iye sadzafuula, kapena kukweza mawu, kapena kupangitsa mawu ake kumveka m’misewu.*

*Bango lophwanyika iye sadzalithyola, ndipo lawi lofuka sadzalizimitsa: iye adzabweretsa chiweruzo kwa choonadi.*

*Iye sadzalephera kapena kukhumudwitsidwa, mpaka iye atayika chiweruzo pa dziko lapansi: ndipo zisumbu zidzayembekezera lamulo lake.*

*Pakuti atero . . . AMBUYE, iye amene analenga miyamba, ndi kuitambasula iyo; iye amene anayala dziko lapansi, ndi . . . amene amatulukamo; iye amene amapereka mpweya kwa anthu amene amakhala pa ilo, ndi mzimu kwa iwo amene amayenda mmenemo:*

*Ine AMBUYE ndakuyitana iwe mu chirungamo, ndipo ndidzagwira dzanja lako, ndipo ndidzakusunga iwe, ndi kukupereka iwe kukhala pangano la anthu, kukhala kuwala kwa Amitundu;*

*Kuti ukatsegule maso akhungu, kuti ukawatulutse mu ndende, kuchokera mu ndende, ndi iwo amene akhala mu mdima . . . kuchokera mnyumba ya ndende.*

<sup>61</sup> Tsopano mu mutu wa 12 wa Yohane Woyera, ndipo tiyeni tiyambire ndi ndime ya 17 ndipo tiwerenge a . . . kutsika mpaka pafupifupi ndime ya 28.

*Anthuwo chotero . . . anali ndi iye pamene iye anamuyitana Lazaro kuchokera mmunda mwake, ndi kumuwukitsa iye kwa akufa, anachitira umboni.*

*Pa chifukwa ichi anthuwo nawonso anakomana naye, pakuti iwo anamva kuti iye anali atachita chozizwitsa ichi.*

*Afarisi chotero ananena kwa wina ndi mzake, Mukuona kuti ife sitipindula kanthu? taonani, dziko likumutsatira iye.*

*Ndipo panali Agriki ena pakati pawo amene anabwera kudzapembedza pa phwando:*

*omwewo anabwera kwa Filipino, amene anali waku Bethsaida waku Galileya, ndipo anamufunsa iye, kuti, Bwana, ife tikufuna timuwone Yesu.*

*Filipo anabwera ndipo anamuuza Andreyo: ndipo kachiwiri Andreyo ndi Filipino anamuuza Yesu.*

*Ndipo Yesu anawayankha iwo, kuti, Ora lafika, limene Mwana wa munthu akuyenera kulemekezeka.*

*Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Pokhapokha njere ya tirigu itagwera mu nthaka ndi kufa, iyo imakhala yokha: koma ngati iyo ifa, iyo imabala zipatso zochuluka.*

*Iye amene akonda moyo wake adzawutaya iwo; ndipo iye amene adana ndi moyo wake mu dziko lino adzawusunga iwo ku moyo wamuyaya.*

*Ngati munthu aliyense anditumikira ine, muloleni iye anditsatire ine; (mvetserani tsopano) ndipo kumene ine ndiri, kumeneko wantchito wanganso adzakakhalako: ngati munthu aliyense anditumikira ine, ameneyo Atate anga adzamulemekeza.*

*Tsopano moyo wanga wavutitsidwa; . . . Ine ndinene chiyani? Atate, ndipulumutseni ine ku ora lino: koma pa (cholinga) cholinga ichi Ine ndinabwera ku ora lino.*

*Atate, lemekezani dzina lanu. Kenako pamenepo panadza liuru lochokera kumwamba, likuti, Ine ndalilemekeza ilo, ndipo ndililemekezanso ilo kachiwiri.*

<sup>62</sup> Tsopano, ine ndikutenga kuchokera mu izi, mutu umene ine ndawugwiritsa ntchito mwanjira yina: *Mabwana, Ife Tikufuna Timuwone Yesu.*

<sup>63</sup> Nthawi m'mbuyomu, ine ndalalikirapo phunziro ili, ndipo, koma mosiyanako pang'ono ndi chimene ine ndikuchifuna, usikuuno. Tsopano, awa ndi mawonekedwe achilendo a zochitika za uthenga wa Khristimasi. Koma ine ndikuganiza, lero, inu, pa wailesi, munamva za *Amuna Atatu Akummawa Ali*, ndi *Mzinda Wawung'ono Wa Betelehemu*, ndi *Usiku Wachete*, ndipo munamva atumiki akuyankhula za kubadwa Kwake, ndi zina zotero. Ndipo ine, poyika Uthenga wanga wa Khristimasi usikuuno, inu mutatha kukhala nazo zochulukira kwambiri za izo masana ano, ndi masiku awiri kapena atatu apitawa, Ine ndinaganiza zoti nditenge mawonedwe osiyana a izo, osati kuchokera ku kubadwa Kwake, ndipo ndiziyankhula izo mwanjira ina. Ndipo kachitidwe kachilendo kwambiri aka, koma ndi mu zinthu zosazolowereka mmene ife timawonamo Choonadi cha Mawu a Mulungu. Izo zimakhala mu chinthu chosazolowereka.

<sup>64</sup> Izo zinali mu kachitidwe kosazolowereka ka Mawu a Mulungu, kuti anthu anamuzindikira Iye kuti anali Mesiya, osati mu kachitidwe kachizolowezi kamene Afarisi ndi Asaduki anabwera nako, kumadzawauza iwo. Ichu chinali chinthu chosazolowereka, kumuwona Mesiya akubadwira mu khola, mmalo mobwera kuchokera mmakonde a Kumwamba, momwe iwo ankaganizira kuti Iye akanadzabwerera, kapena monga iwo—iwo ankanenera kuti Iye akanadzabwerera.

<sup>65</sup> Ichu chinali chinthu chosazolowereka, pamene, pa mtsinje wa Yorodani, pamene “mapiri analumphika monga ana ankosa aang'ono,” ndipo mtumikiyo anatumizidwa patsogolo pa Iye. Mmalo moti iye akhale wansembe wakhalidwe labwino amene akanadzabwera kudzalengeza za kudza Kwake, anamuwona mwamuna ali ndi ndevu pa nkhope yake yonse, ndi tsitsi losapesa, ndipo chidutswa cha chikopa cha nyama chitakulungidwa pa iye, ngati chikhotho. Ndipo akuyenda mmatope, ofika pamwamba pa mapazi ake, mwina mwake, ndipo nkumalalikira uthenga wokondoweza chotero. Ndi kumawauza Afarisi ndi Asaduki, ndipo nkumawatcha ophunzira amenewo, “Inu m'badwo wa njoka.” Izo zinali zosazolowereka kuti munthu achite zimenezo, koma iyo inalinsu njira yopezera Choonadi,

Moyo, njira yosazolowereka. Osati njira yokhazikitsidwa, yachizolowezi, koma njira yosazolowereka.

<sup>66</sup> Ndipo icho ndi chokhumba cha mtima wanga usikuuno, kuti, mu Lemba losazolowereka ili, kuti ife tipezemo tanthauzo lowona la Khristimasi, chimene Khristimasi imatanthauza kwa ife, momwe ife tikuyenera kumachitira izo tsopano, kapena chimene, momwe ife tikuyenera kumachitira pa Khristimasi.

<sup>67</sup> Tsopano ife tikupeza apa, munga ife tawerengera, Agriki awa ankafuna kuti amuwone Iye. Iwo anabwera kuti adzamupeze Yesu. Sindikukayika kuti iwo, munga inu ndi ine, anali atamva za Iye, ntchito zazikulu zimene Iye anali atazichita, ndi kulalikira kopambana kumene Iye anali atachita, ndi zinthu zosazolowereka za moyo Wake, chotero iye anadzakhala Munthu wosazolowereka.

<sup>68</sup> Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyime apa utali wokwanira basi kuti ndinene izi, kuti, pafupifupi nthawizonse, pamene inu mumupeza Mulungu mwa munthu, inu mumapeza munthu wosazolowereka kwambiri akugwiritsidwa ntchito mwanjira yosazolowereka kwambiri.

<sup>69</sup> Kotero, Yesu anali Munthu wa mtundu uwu, ndipo Iye anawakopa anthu, kuti apeze basi chimene Iye anali ndi Yemwe Iye anali.

<sup>70</sup> Ndipo, ndithudi, Agriki awa anali osapembedza, achikunja, chifukwa Agriki ankapembedza mafano. Ndipo iwo anali apamwamba, chabwino, ine ndingati, osema ndi ochita masewero. Ndipo iwo anali ndi zaluso zambiri, Agriki ankatero, luso lalikulu la Chigriki, limene silinaposedwepo ngakhale mpaka lero, pa luso lawo. Ndipo iwo anali anthu apamwamba, ochita zamasewero.

<sup>71</sup> Ndipo pokhala, podziwa kuti kunali Mulungu wina kwinakwake. Ndipo iwo anali nayo masauzande a iyo imene iwo ankaipembedza. Ndipo iwo anali atamva za Mulungu wa mbiriyakale yemwe ankachita zozizwitsa zazikulu pakati pa Agriki. Ndipo kenako iwo anali atamvanso kuti Mulungu uyu, amene anali Mulungu Wachihebri wochita zozizwitsa, anali kumeneko mdziko lawo, ali nawo kenanso. Kotero izo zinakopa tcheru chawo, kotero iwo anabwera kuti adzamuwone Yesu.

<sup>72</sup> Ndipo zindikirani, kawirikawiri momwe anthu amafunira kuti amupeze Yesu, ndi kumupeza winawake amene amadziwa momwe angawatengere iwo kwa Iye. Mtsogoleri, kapena mmodzi wa antchito Ake, ndi momwe iwo amamupezera Iye. Chotero Yesu, ngati Iye amusankha konse wantchito, Iye nthawizonse amamusankha winawake amene angawabweretse anthu kwa Iye, chifukwa ndi cholinga Chake kuti aziwatumikira anthu.

<sup>73</sup> Tsopano ife tikupeza kuti iwo anabweretsedwa mu Kukhalapo Kwake. Tsopano, Agriki awa. Filipo, iwo anali atamufunsa Filipo, ndipo Filipo anati, “Tsopano, apa pali

winawake amene akufuna kuti amuwone Ambuye wathu. Koteri izo sizikanakhala zolondola basi kuti ine ndikhale ndi ulemu woti ndiwawonetse Agriki awa kwa Ambuye wanga, chotero ine ndipita ndikamutenge Andreyi kuti apite ndi ine.” Ndipo chotero iwo anapita ndipo anakamutenga Andreyi. Ndipo Andreyi ndi Filipo, awiri onse, anabwera ndipo—ndipo anawapereka Agriki awa kwa Yesu.

<sup>74</sup> Tsopano, apa pali chinthu chopambana, ndi phunziro limene liri losazolowereka. Basi mwamsanga pamene Agriki awa analozeredwa kwa Yesu, Yesu sanadzilozere kwa Iyemwini, kapena Iye sanadzipangitse Iyemwini kudziwika kwa iwo. Chifukwa, inu simungamudziwe Yesu mwanjira imeneyo. Yesu samadziwidwa mwanjira imeneyo.

<sup>75</sup> Koma mwamsanga pamene, ife tikuwona apa mu Lemba, kuti pamene Agriki awa anabweretsa, anabweretsedwa kwa Yesu, ndipo anali mu Kukhalapo Kwake, izo zikuwoneka ngati kuti Yesu akanati, “Chabwino, izi si . . . Ine—Ine ndi Mesiya wa mtundu wa Chiyuda, zimenezo zakhala zikunenedweratu ndi aneneri, mwa kudzoza, kutsika kudutsa mu zaka mahandirede. Ndipo Ine ndiri pano tsopano. Ndipo Ndine . . . wobadwira ku Nazareti. Ndine wobadwa mwa mayi wa Chiyuda. Atate Anga ndi Mulungu. Ndipo Ine ndiri pano tsopano kuti ndizidziwitse Ndekha kwa inu Agriki.” Tsopano zimenezo zikanakhala zofanana kwambiri ndi kachitidwe ka mu 1961.

<sup>76</sup> Koma, taonani, mwamsanga pamene iwo anabweretsedwa mu Kukhalapo Kwake! Ndicho chinthu chofunikiracho, kuwatengera anthu mu Kukhalapo Kwake. Ndipo mwamsanga pamene anafika mu Kukhalapo Kwake, Yesu anati, “Pokhapokha njere ya tirigu itagwera mu nthaka ndi kufa, iyo imakhala yokha.” Ndi chinthu chosazolowereka bwanji! Mmalola molandira malonje awo, chinthu chimene Iye anachita chinali kuwalozera iwo ku malo amene iwo akanakhoza kukamupeza Iye. “Pokhapokha njere ya tirigu itagwera mu nthaka ndi kufa, iyo imakhala yokha.”

<sup>77</sup> Kodi Iye anachita chiyani apa? Iye anawalozera iwo ku Choonadi chachikulu icho, momwe angamuwonere Iye. Iwo sakanakhoza kumuwona Iye mu njira ya Moyo Wamuyaya, atangoyima pamenepo momwe Iye analiri. Iye anali Munthu.

<sup>78</sup> Mmawa ungapo wapitawo, ine ndinali ndi masomphenya, pafupifupi naini kapena teni koloko mmawa.

<sup>79</sup> Ine ndinali ndikupemphera kwa Ambuye, ndikumverera kuyitana kukundisunthira mosalekeza ku ntchito yakunja chaka chino, kuyambira nthawi yomweyo, mdziko lonse. Ine ndikufuna kuti ndipite ku Norway, ndipo ndikufuna kuti ndipite ku Germany, Africa, ndi ochuluka a mafuko, chaka chino, ngati Ambuye alola. Kuyitana chabe mu mtima mwanga, kuti ndipite.

<sup>80</sup> Ndipo ndinali ndikupemphera kwa Ambuye, ndipo masomphenya anabwera pamaso panga. Ndipo ndinali nditayima pamenepo, ndinayenda ngati chodutsa pansi ndipo ndinalowa mu—mchipinda mmene munali akazi awiri, makamaka. Mmodzi anali pa kauntala, ndipo winayo anali pa kauntala. Iwo anali akugulitsa zinthu zosiyanasiyana. Chabwino, ine ndinaima kwa mphindi ndipo ndinali ndikudabwa chimene izo zinali. Kenako ine ndinamuwona mwamuna akubwera mmenemo, ndipo iye anagula kwa mkazi wa pa kauntala *iyi*, botolo laling’ono la zonunkhiritisa limene linkapita kwa wina, mkazi wake, mwinamwake.

<sup>81</sup> Kenako ine ndinayenda kupitapo, ndipo ine ndinati, “Zonunkhiritisa izo mukugulitsa ndalama zingati? Ndikufuna zina za mkazi wanga, koma ndikufuna za lilac. Ndimakonda ma lilac.”

<sup>82</sup> Ndipo iye anati, kapena mkaziyo anati, kani, a . . . “Botolo laling’ono ili limene mwamuna uja anamugulira mkazi wake, ndi la masenti forte, koma si lilac. Botolo lina ili, la lilac, ndi la dola imodzi ndi masenti nainte eyiti.”

<sup>83</sup> Ndipo ine ndinati, “Ine nditenga limenelo.” Ndipo ine ndinapita ku kachikwama kanga, kuti ndikatenge ndalama. Ndipo ndimaganiza kuti ndinamupatsa iye ma wani dolla awiri.

<sup>84</sup> Pondibwezera, iye anati, “Bwana, ine sindikuidziwa ndalama iyi.” Ndipo iye anaibweza iyo kwa ine. Ndipo iyo inali faivi dolla yaku Canada.

<sup>85</sup> Ndipo ndinati, “Mundikhululukire ine. Ine ndimaganiza kuti iyo inali dolla.” Ine ndinati ndiye, “Ine ndi . . . Ndine mmishonare. Ndipo ine, mu utumwi wanga, ine ndimapeza ndalama kuchokera ku madera osiyanasiyana a dziko lapansi. Ndipo, potero, ine ndinalakwitsa.”

<sup>86</sup> Koteri, iye anandibwezera faivi dollayo. Ndipo ine ndinamupatsa iye wani dolla yaku America. Ndipo iye anandipatsa ine chenje, ndipo iye anati, “Mishonare?”

Ndipo ine ndinati, “Inde, amayi.”

<sup>87</sup> Ndipo pamene ine ndinali kuyankhula, kapena ndikuyang’ana pa iye, iye anadzayang’ana kwa mkazi winayo, ndipo iye anakhala ngati anagwedeza mutu wake. Ndipo iye anati, “Wokondedwa, kodi iwe ukukhulupirira kuti M’bale Branham akulondola, kuti ife akazi lero tikuyenera kumakhala monga iye anatiwuzira ife, ndi kudula kwa tsitsi lathu, ndi kavalidwe ka zovala zathu, ndi zinthu monga chomwecho?” Anati, “Kodi iwe sukuganiza kuti iye akulakwitsa mu zimenezo?”

<sup>88</sup> Iye anati, “Inde.” Ndipo iye anati, “Zipitirira, wokondedwa. Iwe, Ruth,” kapena chirichonse chimene dzina lake linali; anati, “iwe uli ndi kudzoza. Zinene izo.”

<sup>89</sup> Chabwino, mwamsanga, ine ndinadziwa kuti ine ndinali mmasomphenya, chotero ine ndinadziwa kuti awo anali akazi awiri amenewo, nthawizonse. Mukuona? Iwo ali, awiri onse, aumodzi ndi mpingo wautatu. Apo iwo anayima pamenepo.

<sup>90</sup> Ndipo anati, “Inde.” Anati, “Ine sindikuganiza kuti ife tikuyenera kumatero. Chifukwa, ife sitinawawonepo maso Ake. Ife sitinawawonepo mapangidwe Ake. Ife sitingadziwe momwe Iye ankawonekera, kotero chifukwa chiyani kuti ife tizichita zimenezo?”

<sup>91</sup> Ndipo ine ndinali nditavala suti yolondera. Ndipo ine ndinati kwa mkaziyo, ine ndinati, “Mphindi yokha, alongo anga. Mwaona, inu mukuyenera kumakhala basi mogwirizana ndi Baibulo, ziribe kanthu momwe Izo zinaliri.”

<sup>92</sup> Iye anati, “Koma ife sitinakhalepo konse kumbuyo uko, ndipo ife sitinamuwonepo konse Iye.”

Ine ndinati, “Ine ndinamuwonapo Iye.” Ndipo ine ndinati, “Chinthu chake ndi chakuti. . .”

<sup>93</sup> Ine ndinaganiza, “Ambuye, tsopano, ine ndiri pamaso pa mipingo iwiri yayikulu, yanzeru. Tsopano, Inu mukuyenera kuti mundipatse ine nzeru.”

<sup>94</sup> Ndipo chotero ndiye ine ndinadzimva ndekha ndikuyamba kuyankhula. Ine ndikufuna kuti inu muzifufuze izo. Sindinaganizirepo konse za izo, m’moyo wanga. Ine ndinati, “Munthu lero akuyenera kukhala monga iye analiri nthawi imeneyo, chifukwa iye ndi munthu yemweyo. Iye ndi wopangidwa ndi zokhudzira zisanu. Ndipo ngati iye atayima ndi kuyang’ana pa Iye, pa nkhope pomwe, iye akanayenerabe kukhala ndi chokhudzira cha chisikisi cha chikhulupiriro chimenecho, kuti amukhulupirire Iye, ziribe kanthu momwe Iye ankawonekera. Iye akanayenera kuti amukhulupirire Iye, mulimonse.”

<sup>95</sup> Ndipo iwo anabisa nkhope zawo ndi manyazi, ndipo anati, “Ife sitinaziwonepo konse izo, bwana, monga choncho,” ndipo anayamba kuchokapo. Kenako ine ndinatembenuka ndipo ndinayamba kupita ku utumiki wa umishoni, chimene ndikudziwa kuti kunali a—a—kuyitana kondibwezeretsa ku utumiki.

<sup>96</sup> Tsopano, onani, Iye anawalozera, iwo pamenepo mu Kukhalapo Kwake, Khristu anawalozera iwo ku Choonadi. Iye ananena momwe angamuwonere Iye, anali woti apite ku mtanda. Kumeneko ndi kumene izo zimachitikira, pa mtanda. “Pokhapokha njere ya tirigu itagwa, iyo imakhala yokha.” Ndipo ngati Iye akanati asafe, Iye akanati—akanayenera kukhala yekha, Mwiniwake, ngati Iye akanati asafe. Koma, Iye, pokhala njere ya tirigu imene inagwera mu nthaka. “Ndiyeno ngati iyo igwera mu nthaka,” Iye anati, “iyo idzabala zochuluka, ngati iyo igwera mu nthaka ndi kufa.” Choyamba, iyo ikuyenera

kukhala njere yamoyo, apo ayi iyo singabale kanthu. Koma iyo ikuyenera kukhala ndi moyo mwa iyo iyo isanagwere mu nthaka. Ndipo Iye anali ndi Moyo Wamuyaya mwa Iye, chifukwa Iye anali Emanuele. Ndipo Iye ankayenera kuti apereke Moyo Wake Womwe, ndi cholinga chakuti abweretsenso Moyo kachiwiri.

<sup>97</sup> Titenge, monga tiriguyo. Inu mukuti, “Zingatheke bwanji kuti njere imodzi ya tirigu?” Ichi ndi chimene chimachitika. Njere imodzi ikagwera mmenemo, iyo imabala njere handirede. Njere handirede zikagwera mmenemo, zimabala njere sauzande. Mbewu sauzande zikagwera mmenemo, ndipo zimabala mbewu milioni. Mbewu milioni zikagwera mmenemo, ndipo zimabala a—katundu wapa ngolo. Ndi kumapitirira, ndi kumapitirira, ndi kumapitirira, mpaka izo zimadyetsa dziko lonse.

<sup>98</sup> Ichu ndi chimene Iye ankatanthauza. “Ngati Ine ndingawukhale Moyo Wangawu ndekha, ndi kufa mwanjira iyi, Ine ndidzangowukhala Moyo Wangawu ndekha, chabwino, ndiye, sipadzakhala chipatso pambuyo pa Ine. Koma ngati ndigwera mnthaka, pansu pa chifuniro cha Mulungu, ndipo ine ndidzabweretsa Kubadwa kwatsopano. Ndipo kudzera mu Kubadwa kwatsopano kumeneko, iko kudzabala Kubadwa kwatsopano kwina, ndi Kubadwa kwatsopano kwina, mpaka dziko lonse, lidzatumikiridwa; lidzalalikiridwa ndi Uthenga.” “Uthenga uwu ukuyenera kulalikiridwa ku dziko lonse lapansi, ngati umboni kwa Ine. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

<sup>99</sup> Koteru ngati ife eniake ndiye, mu utumiki wathu, ndi m'malingaliro athu, ndi m'moyo wathu, ngati ife tikhala monga ife tiririmu, ife sitidzachita ubwino uliwonse. Ife tikuyenera kufanso pa guwa, apo ayi tidzakhala tokha; ife tidzakhala tikukhala moyo wa chipembedzo china kapena kachikhulupiriro kena; ife tidzakhala tikukhala moyo wa bungwe linalake. Koma ngati ife tifa kwa ifeeni, ndiye Mzimu Woyera udzafalitsidwa paliponse, ndi milomo yathu. Ife tikuyenera kufa. Ochuluka kwambiri, lero, momwemonso izo ziri monga pano. Kuti ngati. . . Ife tikuyenera kuzindikira kuti ife tikuyenera kuti tife, ndi cholinga chakuti tibweretse moyo watsopano. Chotero Iye ananena zochuluka kwambiri mu izi, “Ngati inu mukufuna kuti muniwone Ine, inu mukuyenera kufa. Mufe kwa inueni, ndipo mukatero inu mudzabala moyo watsopano.”

<sup>100</sup> Tsopano, ngati ife tikufuna kuti timuwone Iye, ngati inu mungayembekezere konse kuti mudzamuwone Iye, inu simudzamuwona konse Iye mwa kujowina mpingo, bukhu lina la malamulo limene inu mumalisunga, tizikhulupiriro tina timene inu mumatitumikira. Inu mudzamuwona Iye pamene inu mudzafa. Pamene inu mudzabwera pa Kalvare ndi kudzapachikidwa kwa inueni, ndiye inu mudzamuwona Yesu. Ife tidzamuwona Iye.

<sup>101</sup> Choyamba, Iye asananene chirichonse, Iye anawalozera iwo ku malo oti akamupeze Iye. Monga Amitundu onse, kapena anthu onse, inu mumamupeza Yesu pa mtanda, pamene inu mumapachikidwa ndi Iye.

<sup>102</sup> Lero, ife timayesetsa kuti timupeze Iye mu chirichonse. Ife timayesetsa kuti timupeze Iye mu nyumba ya tchalitchi. Ife timayesetsa kuti timupeze Iye mu chipembedzo. Ife timayesetsa kuti timupeze Iye ponena kachikhulupiriro kenakake. Ife timayesetsa kuti timupeze Iye posunga masiku enaake, pomvera miyambo inayake. Koma ife sitingamupeze, mpaka ife titafika ku Kalvare. Apo ife timapachikidwa, timagwera mu fumbi la dziko lapansi, ndi kufa kwa ifeeni, kenako nkubadwanso kachiwiri. Zikatero ife timamupeza Yesu.

<sup>103</sup> Oh, ambiri akumayesetsa, lero, kuti adzigwire okha ndi kusungabe lingaliro lanu. “Ine ndiri ndi njira *yanga* ya izo. Ine ndimakhulupirira *izi*.” Koma inu simungamupeze Khristu mpaka inu mutafa kwa inueni, ndi kumulandira Iye, Mawu, mukatero inu mumapeza Moyo. Tiyeni tiwone.

<sup>104</sup> Ndi zosiyana bwanji lero! Ndi zosiyana bwanji lero, lero, ndi mipingo, kapena ophunzira a lero! Kodi iwo amachita chiyani, ngati inu mubwera kwa ophunzira lero?

<sup>105</sup> Ophunzira amenewo, iwo asanachite chirichonse, iwo anawatengera Agriki awa mpaka mu Kukhalapo komwe kwa Yesu. Ndipo ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye adzayenera kuti adzachite zomwezo lero ngati inu mutabweretsedwa mu Kukhalapo Kwake.

<sup>106</sup> Ophunzira lero ndi osiyana kwambiri, kwa lero. Iwo amayesetsa kukutengerani inu ku khola, kapena modyera ng’ombe, kapena kwa Santa Claus, kapena kwa kalulu wa Isitara, kapena chinachake chimzake, mmalo mwa Khristu. Iwo samakubweretsani inu mu Kukhalapo kwa Khristu. Khrisimasi si Khristu. Ayi. Lero, iwo amakubweretsani inu, ku malo ena, ku chosema china, mpingo wina, bungwe lina, malamulo ena a chiphunzitso, koma osakutengerani inu mu Kukhalapo kwa Khristu.

<sup>107</sup> Wophunzira weniweni, woona angakubweretseni inu molunjika kumene mu Kukhalapo kwa Khristu. Ndipo kuchokera pamenepo, Khristu angakusonyezeni inu zomwe inu mumayenera kuchita.

<sup>108</sup> Tsopano, “Mzimu wachoka mu Khrisimasi,” winawake anatero lero. Ine ndinawamva iwo pa walesi, anatero munthu akupereka chitsutso, mtumiki, za, “Anthu ambiri lero akuti, ‘Khrisimasi si *ichi*. Ndipo ife sitimayenera kukhala ndi Santa Claus ndi zinthu.’” Ndipo munthu ameneyo amayesetsa kupanga mfundo zake kuti zimveke bwino, akuti, “Ngati inu munamuchotsa Santa Claus mu Khrisimasi, inu munachotsa

mzimuwo.” Inu munachotsa mzimu wa Santa Claus, izo ndi zoon. Ndipo mzimu wa Santa Claus si. . .

<sup>109</sup> Santa, nthano ina yaku Germany, mwambo wachi German wa Katolika, si mzimu umene umapanga Khrisimasi. Mzimu umene Khristu analozera ku unali Mzimu Woyera, umene siuli chikondwerero, koma kupembedza kwa Mulungu wamoyo.

<sup>110</sup> Koma iye anati, “Inu mukachotsamo Santa Claus, simukhalanso mzimu mu Khrisimasi.” Kodi inu mungalingalire mtumiki akunena zimenezo pa wailesi? Koma ndicho chimene iye ananena, anati, “Inu mukachotsa Santa Claus, ndipo inu simukhalanso ndi mzimu wa Khrisimasi.” Chabwino, zikhoza kukhala zomwezo, pogwiritsa ntchito mawu oti *misa ya Khristu*, inu mukhoza osakhala ndi zochuluka za izo.

<sup>111</sup> Koma mukamuchotsamo Santa Claus mmoyo wanu, mutsegule mtima wanu ndipo mumulole Khristu alowemo, mufe kwa zinthu izi za mdziko, ndi cholinga choti mukhale ndi Khrisimasi yenyeni. Inde.

<sup>112</sup> Ndi zosiyana kwambiri, ndi momwe izo zinkakhalira, koma izo zinasintha. Osati—osati, Khristu sanasinthe. Ophunzira lero ndi osiyana kwambiri ndi ophunzira akale. Lero, ophunzira amabweretsa oyankhula, kapena ofunafuna, kani, mmalo mwa. . . Ophunzira akale ankamubweretsa wofunafunayo mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ndipo lero, ophunzira a lero, akuwabweretsa iwo mu kukhalapo kwa bungwe linalake la mpingo, chiyanjano chinachake, kachikhulupiriro kenakake, chiphunzitso chinachake, mmalo mowabweretsa iwo mu Kukhalapo kwa Khristu.

<sup>113</sup> Ife titenge mawu akuti *Khrisimasi*. Inu simumamva kawirikawiri Dzina la Khristu likutchulidwa. Inu simumamva Ilo likutchulidwa. Kuwala ndi zonyezimira zonse ziri pa Santa Claus, osati pa Khristu, mpaka anthu samadziwa nkomwe kuti Khrisimasi kwenikweni ndi yandani. Iwo angochipanga icho kukhala chachikunja ndi kuchipanga icho chachikunja, mpaka icho chonse chasanduka chachikunja. Ndi tsiku lalikulu lazamalonda a zikondwerero. Tsopano, ngati iwo akufuna kuti apange tsiku lamalonda monga tsiku la anakubala, kapena tsiku la abambo, kapena tsiku la mwana wamwamuna, kapena tsiku la mwana wamkazi, izo nzabwino bwino. Koma muchotsemo zamalondazo mu Khrisimasi. Ine ndinawona chikwangwani osati kale kwambiri, chinati, “Mubwezeretseni Khristu mu Khrisimasi.”

<sup>114</sup> Tsopano, iwo amakubweretsani inu ku tchalitchi, inu mumakaphunzira kachikhulupiriro. Iwo amakubweretsani inu ku Khrisimasi, inu mumakachita chiyani? Inu mumakawona Santa Claus. Iwo amakubweretsani inu ku tchalitchi, inu mumakawonako bungwe.

115 Koma Khristu anawabweretsa iwo ku mtanda. Ndipo pamene inu mumupeza wophunzira weniweni amene angakulozereni inu kwa Khristu, Khristu adzakubweretsani inu ku mtanda, kumene inu mumapachikidwa ndi Iye. Ndipo Moyo Wake Wamuyaya ndi moyo wanu umakumana pamodzi, ndipo moyo wanu umafa, ndipo inu mumatenga Moyo Wake Wamuyaya, ndipo zikatero inu mumakhala mwana wa Mulungu. Amen.

116 Ndi kusiyana kotani, kwa wophunzira wakale ndi wophunzira wa lero!

117 Ngati mutatchula kwa wophunzira kuti, “Ine ndikufuna ndimudziwe Ambuye Yesu.”

118 “Chabwino, tsopano taonani, ife ndi a mpingo *wakuti-wakuti*, mubwere kuno ndipo mudzajowine umenewo, mudzatiwowine ife.” Mukuona? Kapena, “Ife tinali...Ife ndi a gulu *lakuti-lakuti* ili, ndipo bwerani mudzajowine *ilo*.” Ndipo izo ndi zimene inu mumazimva.

119 Koma Khristu Mwiniwake anawalozero anthu ku imfa Yake, ndipo anati, “Pokhapokha njere ya tirigu itagwera mu nthaka, iyo imakhala yokha.”

120 Oh, izo ndi zosiyana bwanji! Inde, bwana. Ndi zosiyana bwanji! Koma moyo wanu ndi Moyo Wake umapezana wina ndi umzake, osati pa tchalitchi, osati mnyumba, osati mu kachikhulupiro, osati mu ntchito zabwino, koma pa mtanda pamene inu mumapachikidwa ndi Iye. Pamenepo ndi pamene inu mumamupeza Khristu. Inu simumamupeza Iye pa kuchita bwinoko, kutsegula tsamba latsopano. Kuyamba moyo watsopano, inu simumamupeza Khristu. Inu mumamupeza Khristu mu imfa yokha; osati modyera ziweto, osati mu kuvomereza. Kukhulupirira mu tizikhulupiriro tinatake ndi nthano, inu simumamupeza Khristu mmenemo.

121 Wantchito woona amakutengerani inu kwa Iye, ndipo Iye ndi Mawu. Inu mukuti, “Ndiye, M’bale Branham, ngati Khristu ali pa dziko lapansi lero, wantchito weniweni angamutengere iye kwa Iye, Khristu.” Chabwino, Khristu ali pano, mmawonekedwe a Mawu. Ndipo Mawu amabweretsa Moyo, chifukwa Iye ndi Mawu. Khristu ndi Mawu. Inde, bwana. Iye ndi Mawu, Iyemwini. Wantchito woona nthawizonse amakutengerani inu ku Mawu.

122 Tsopano, Iye ndi Mawu. Iye ndi Baibulo ili litapangidwa kukhala moyo. Ndipo pamene inu mufa kwa inumwini, ndi Khristu, monga njere ya tirigu, ndiye Mawu amakhala moyo mwa inu, amabweretsa zotsatira zomwezo monga Iwo anachitira mu mbewu ya tirigu yamoyo Ija imene inkayenera kugwera mu nthaka. Amen. Ndinu ogawana nawo mu chiwukitsiro Chake. Ndinu ogawana ndi Iye, mu madalitso Ake onse, mu mawonetseredwe Ake onse. Ndinu ogawana ndi Iye, mu zonse zimene Iye anazichita.

Tsopano, Iye ndi Mawu ndi kutanthauzira Kwake kowona.

<sup>123</sup> Tsopano inu mukuti, “Oh, ife timakhulupirira Baibulo, bwana. Ife timakhulupirira Baibulo.”

<sup>124</sup> Koma tsopano, ngati inu mumakhulupirira Baibulo, Yesu ananena izi mu Baibulo, Yohane Woyera 14:12, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita.” Uko ndiko kutanthauzira kowona kwa Baibulo, pakuti Mulungu Mwiniwake ali mwa inu, akuyankhula moyankha kutanthauzira Kwake Komwe. Ulemelero! Uko ndiko kutanthauzira kowona, Mulungu mwa inu, akutanthauzira Mawu Ake Omwe. Amen. Kodi Yesu sanati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira”? Mulungu mwa inu, akupereka kutanthauzira Kwake Komwe. Inu simumasowa kuti muziyang’ana kwa winawakenso. Nkumati, “Mawuwo akunena *ichi*.” Khulupirirani Iwo, ndipo Iwo adzazitanthauzira Okha, chifukwa ndi Mulungu akukugwiritsani inu ntchito kuti mutanthauzire Mawu Ake Omwe. Amen. Khristu ndi kutanthauzira kwamoyo kwa Mawu Ake Omwe.

<sup>125</sup> Tiyeni tiyang’ane pa ena, momwe Iye amawatanthauzira Mawu, tsopano, ngati Iye ali ndi kutanthauzira kolondola.

<sup>126</sup> Tsopano tikapita kumusi kuno kwa Amethodisti, iwo amati, “Ife tiri nako kutanthauzira kolondola.” Abaptisti, iwo amati, “Ife tiri ndi kutanthauzira kolondola.” Apresbateria, “Ife tiri nako kutanthauzira kolondola.” Mpingo wa Khristu, wotchedwa chomwecho, “Ife tiri nako kutanthauzira kolondola.” Onse a iwo ali nako “kutanthauzira kolondola”? Iwo onse ndi osiyana, wina ndi mzake. Ndiye, pali chinachake cholakwika penapake.

<sup>127</sup> Tsopano, njira yokhayo imene ife tingapezere, ndi kupeza njira imene Yesu anawauza Ayuda momwe angatanthauzire Mawu. Amen. Ndipo ngati Khristu ananena chomwecho, izo zimapangitsa izo kukhala zolondola.

<sup>128</sup> Amethodisti amati, “Momwe abale athu amatanthauzirira Iwo, bungwe.” Abaptisti amati, “Momwe ife timawatanthauzirira Iwo.” Apresbateria amati, “Momwe ife timawatanthauzirira Iwo.”

<sup>129</sup> Koma ndi momwe Yesu anawatanthauzirira Iwo, uko nkulondola. Tiyeni tiwone momwe Iye anawatanthauzirira Mawu. Iye anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Mawu a Atate Anga, musandikhulupirire Ine.” Izo zikukhazikitsa izo. Umo ndi momwe Iye ankawatanthauzirira. Iye anati, “Ngati inu simungandikhulupirire Ine, mukhulupirire ntchito zimene Ine ndazichita. Ndipo ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, musakhulupirire izo, nkomwe.” Amen. Izo zikukhazikitsa izo.

“Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita.”

<sup>130</sup> Tsopano, pakuyenera kukhala chinachake cholondola ndi chinachake cholakwika. Kapena, mwina, kodi ife tikuchita chiyani? Kodi ife tikusewera ndi chiyani? Kodi ife tikutani, kumapita mozungulira kuno, kumanyengezera kukhala Akhristu, ndi kumachita *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*, ndi kumajowina tizikhulupiriro *iti*, ndi kumagwirana chanza ndi mtundu *uwu* wa Pentekoste, kapena *uwo*, kapena Amethodisti, kapena Apresbateria, kapena Abaptisti, kapena Akatolika? Kodi zonsezo ndi za chiyani? Kodi ife tikuchita chiyani, kusewera chibisalirano, mphaka ndi khoswe? Kodi ife tiri pati?

<sup>131</sup> Ndiye ilipo njira imodzi yokha, maziko amodzi okha. Ilipo njira imodzi yokha yotsimikizika, ndiko kutanthauzira kumene Yesu anapereka ku Mawu. Aleluya! Ndiko kutanthauzira kumene kuli kolondola. Anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito zimene Mulungu anati Ine ndikanadzazichita, ndiye musandikhulupirire Ine.” Amen. Uko ndiko kutanthauzirako.

<sup>132</sup> Kutanthauzira lero ndi, Yesu anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zomwezo zimene Ine ndikuzichita nayenso adzazichita.” Ndipo Lemba nalonso linati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Yesu anati, “Umo ndi momwe mungadziwire ngati Ine ndinachokera kwa Mulungu kapena ayi.” Ndi momwe mungadziwire.

<sup>133</sup> Iwo anati, “Tsopano, dikirani miniti. Ife tiri naye Abrahamu, atate athu.” Iye anati, “Makolo athu ankadya manna mu chipululu.”

Ndipo Yesu anati, “Iwo onse anafa.”

“Ife tinamwa madzi kuchokera mu thanthwe lokanthidwa.”

“Ndipo iwo onse anafa.”

<sup>134</sup> Anati, “Koma Ine ndi Mkate wa Moyo umenewo umene unkabwera kuchokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba.” “Ndipo si Ine amene ndikuyankhula, ndi Atate Anga amene akukhala mwa Ine. Iye ndi Wotanthauzira wa Mawu Auzimu amenewo. Ndipo Iye akutsimikizira kachiwiri kuti Iye ndi Mulungu, chifukwa Iye akuchita ndi Ine zimene Iye anati Iye akanadzazichita.” Amen. Ndiro Lemba.

<sup>135</sup> Umenewo ndiwo Uthenga woti udzifika kwa anthu; osati chikuta, osati modyera ziweto. Khristimasi simatchulidwa mu Bukhu lonse la Mabaibulo. Palibe nthawi imodzi imene Yesu anawalozerapo iwo ku kubadwa Kwake, koma ku imfa Yake.

<sup>136</sup> Palibe nthawi imodzi imene Yesu anayamba wanenapo kuti, “Jowinani mpingo.” Palibe nthawi imodzi imene Iye anayamba wayankhulapo kuti, “Bwerezani kachikhulupiriro.”

<sup>137</sup> Koma Iye anati, “Bwerani kwa Ine.” Ndipo Iye anati, “Iye amene adzabwera, ntchito zimene Ine ndikuzichita zidzamutsatira iye basi monga momwe izo zikuchitira ndi Ine.”

138 “Pakuti ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate, musandikhulupirire Ine. Chifukwa, Mawu anati, pamene Mesiya adzabwera, zinthu izi zizidzachitika. ‘Iye adzakhala mneneri.’ Inde. ‘Iye akanadzakhala mneneri. Iye akanadzakhala mpenyi monga momwe Mose anali.’ ‘Olumala akanadzalumpha ngati nswala. Akhungu akanadzawona. Ogontha akanadzamva. Ndipo osayankhula akanadzayankhula. Izo zikanadzawonetsera, mwa Iye, momwe Iye akanadzachitira zizindikiro za Mesiya.’ Tsopano, ngati zizindikiro za Mesiya sizikutsimikizira utumiki Wangwa,” Iye anati, “ndiye musandikhulupirire Ine. Koma, umu ndi momwe inu mumatanthauzirira Mawu.” Iye anati, “Ngati Ine ndiribe zizindikiro izi, ndiye musakhulupirire izo. Koma ngati Ine ndikuwonetsera zizindikirozo, ndipo inu simukundikhulupirira Ine potanthauzira Mawu, mukhulupirire zizindikirozo, pakuti izo zikuyankhula za Mawu.” Uko ndiko kutanthauzira kwenikweni kwa Iwo. Ndi zimenezotu. Ndiwo Uthenga.

139 Inu simukuyenera kuti muzitenga mawu a wina aliynse. Inu simukuyenera kuti muzijowina mpingo uliwonse. Inu simungajowine Mpingo. Inu mukhoza kujowina mabungwe awa. Koma Mpingo wa Mulungu, inu mumabadwira mwa Iwo, kuchokera ku Kalvare.

140 Mukuti, “Mulungu adalitsike! Ine ndiri, nanenso, M’bale Branham.” Ndiye ntchito zimene Yesu ankazichita, inunso mudzazichita. Ndi zimene Yesu ananena. Mukuona? “Ntchito zimene Ine ndikuzichita...” Chiyani? Iye anati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita, zikuchitira umboni za Ine.” Aleluya! “Ntchito zimene Ine ndikuzichita, zikuperekeramba umboni.” Kodi inu simukuona? Mwa kuyankhula kwina, “Zizindikiro za Mesiya, kodi inu simukuwona zimene Mesiya amayenera kuti adzachite? Ndipo inu simukukhulupirira kuti Ine ndiri ndi kutanthauzira kolondola kwa Mawu, ndiye nchifukwa chiyani Atate Anga akuyikira izo kumbuyo? Inu mukuganiza kuti ine ndikulimbisa kwambiri pa mabungwe anu,” Iye anati, “ngati inu mukuganiza kuti ndine—wotsutsa kwambiri. Ndipo inu mukuti Ndine ‘munthu wamisala,’ Ine ‘ndiri ndi mdierekezi,’ ine ndasokonezeka mmalingaliro Anga.”

141 Iwo anamuuzira Yesu kuti Iye anali wamisala. *Wamisala* zimatanthauza “wopenga.” “Ndiwe wopenga. Iwe si wamagulu athu. Ndipo Iwe uli kunja kuno ngati munthu wamisala. Iwe wasokonezeka mmalingaliro Ako.”

142 Ndiye Yesu akanakhoza kunena kwa iwo, ichi, “Ndiye ngati inu muli a Mulungu, zizindikiro za Mulungu ziri kuti? Ngati inu mumakhulupirira mwa Mose, zizindikiro za Mose ziri kuti ndi inu? Ngati inu mumakhulupirira mwa aneneri, chizindikiro cha aneneri chiri kuti ndi inu? Koteri ngati simungakhulupirire kuti Ine ndiri ndi kutanthauzira kolondola, khulupirirani zizindikirozi, pakuti Izo zikuchitira umboni kuti

Ine ndikulondola.” Aleluya! “Izo ndi zimene zikuchitira umboni za Ine. Izo zikuchitira umboni ngati Ine ndikulondola kapena ayi. Onse amene Atate anandipatsa Ine adzatsatira Izo ndipo adzabwera kwa Izo. Ndipo palibe munthu amene adzakhoze kubwera pokhapokha Atate atamuyitana iye.” Kulondola.

<sup>143</sup> Komabe, “Iye anali atachita ntchito zochuluka kwambiri,” Baibulo linati, “komabe iwo sanamukhulupirire Iye, chifukwa Yesaya anati, ‘Iwo ali nawo makutu ndipo sakutha kumva; maso ndipo sakutha kuwona.’” Iwo anali akhungu ngati mleme. Komabe, iwo sankatha kuziwona izo, chifukwa mneneri anati iwo sakanakhoza. Tsopano, chinthu chomwecho chiri lero monga zinaliri nthawi imeneyo. Eya.

<sup>144</sup> Anati, “Ngati inu simungathe. . . Ine sindikuchita ntchitozo. Si Ine amene ndikuchita, ndikuyankhula Mawu. Si Ine amene ndikuchita ntchitozi, mwanjira ina. Ndi Atate Anga. Ndipo ngati inu mukudziwa chimene Mulungu anali, Mulungu anali Mlengi. Mulungu anali Mmodziyo amene anali pa Mose, ndipo Mulungu mwa Mose ananeneratu za tsiku Langa. Mulungu anali mu Chipangano Chakale,” Iye anatero. Zochuluka kwambiri monga kunena kuti, “Iye amene anali mwa aneneri, anakuuzani inu kuti, ‘Mneneri Wamkulu uja akanadzabwera tsiku lina, ndipo kwa Iye anawo akanadzasonkhanitsidwa.’ Ngati inu simungathe kukhulupirira momwe Ine ndikutanthauzirira Mawu kwa inu, ndiye mukhulupirire zizindikirozi, pakuti izo zikuyankhula za Ine.”

<sup>145</sup> Oh, iwo sanakhulupirire. Iwo, iwo sanathe kuziwona Izo. Iye anali Mulungu mu thupi. Chifukwa, kodi Iye anali chiyani? Iye anali Mawu owonetseredwa. Iye anali chimene Mulungu anali atalonjeza.

<sup>146</sup> Mvetserani, Branham Tabernacle. Mudzimangire nokha, pa usiku wa Khristimasi uwu. Mukuona?

<sup>147</sup> Ngati Iye sanali, ndiye Mulungu sakanamutsimikizira Iye. Ndithudi. Mwa kuyankhula kwina, Iye akanakhoza kunena kuti, “Ndi liti mwa magulu anuwo (Afarisi, Asaduki, kapena chirichonse chimene iwo akanakhoza kukhala), ndani mwa anthu anuwo, ndani mwa akulu ansembe anuwo, ndani mwa ophunzira anuwo, amene Mulungu amamugwiritsa ntchito kuti ayankhuliremo Mawu Ake ndi kuwawonetsera Iwo, kunena kuti Iwo akulondola?”

<sup>148</sup> Chabwino, iwo akanakhoza kunena kuti, “Amuna athu ndi ophunzira. Ndife anzeru. Ife timalidziwa Baibulo limenelo kuchokera ku m’badwo kupita ku m’badwo.”

<sup>149</sup> “Chabwino, ndiye, nanga bwanji Mulungu sakuwapanga Iwo kukhala amoyo kachiwiri mwa amuna amenewo, ngati Iwo ali Mawu a Mulungu?”

<sup>150</sup> Taonani. “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi,” osati atatu. “Ndife Mmodzi.” Mulungu anali mwa Iye. Mulungu

ankayankhula kudzera mwa Iye. Iye salinso Iyemwini, koma Iye ndi Liwu la Mulungu kupyolera m'milomo ya munthu. Aleluya!

<sup>151</sup> Ndipo wokhulupirira aliyense yemwe ali mwa Iye, usikuuno, nayenso ndi wodzazidwa, wodzazidwa kwambiri, wogonjera kwathunthu, mpaka kuti mawu ake amakhala ngati Mawu a Khristu. Iye akayankhula ndipo Mawu amasandulika thupi. Iye akayankhula ndipo Mawu amawonetseredwa. “Ntchito zimene ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

<sup>152</sup> Yesaya ananena, mu mutu wa 42, ife tangowerenga kumene, “Kuwala kwakukulu kwabwera.” Kuwala! Oh, ine sindikufuna kuti ndichoke pa phunziroli. Koma Kuwala kwakukulu kwambiri kumene kunayamba kwawalapo kunawala mwa wodzichepetsa uja, Mnazareni wamng’ono: Munthu wopanda kukongola koti ife timukhumbire Iye; Mwamuna wopanda maphunziro, momwe dziko limayankhulira; Munthu amene sankadziwa miyambo ndi zinthu za mdziko lino. Koma ankakhoza kumanga ziwanda, kuwukitsa akufa, ndipo adierekezi ankanjenjemera.

<sup>153</sup> Ndipo Mulungu anamuzindikira Iye kuchokera Kumwamba, ndipo anayankhula mobweza kuti, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa.” Osati pamaso pa anthu apamwamba, koma pamaso pa gulu losankhidwa limene Iye anali ataliyitana. Kuwala Kwakukulu!

<sup>154</sup> Bwanji? Kuwala kwakukulu kunkawala kuchokera ku Mawu Ake. Kodi Mawuwo anali chiyani? Khristu. Iye anali chiyani? Mawu atabweretsedwa ku Moyo. Ndipo Mawu atabweretsedwa ku Moyo, anapereka Kuwala kwakukulu kuposa momwe Iye anachitira pamene Iye anati, “Kuwale,” mu Genesis 1. Kumeneko kunali kuwala kwa chirengedwe, chirengedwe chachivundi, chimene chikuyenera kugwa. Koma Mawu Ake anali Moyo Wamuyaya ndi Kuwala Kwamuyaya. Ndipo pamene munthu anakhulupirira Zimenezo, iye anali ndi Kuwala Kwamuyaya.

<sup>155</sup> “Kuwala kwa iwo amene akukhala mmadera a mithunzi ya imfa,” Mateyu 4. “Kubweretsa Kuwala kwa Amitundu,” amene anagwidwa ndi kutsutsidwa ndi Mulungu, mu mafano awo. Koma Iye anadzabwera ngati Kuwala.

<sup>156</sup> Kodi iye ananena chiyani? “Mawu Anu ndi Kuwala ku njira yanga, Kuwala kuti kuwunikire njira kwa anga—ku mapazi anga, kuti kundilondolere ine.”

<sup>157</sup> Ndipo lero, Kuwala kwa Mulungu ndi Mawu a Mulungu owonetseredwa, Kuwala kukuwonetseredwa. Kuwala ndi ntchito za Mulungu, zoyankhulidwa ndi Mawu a Mulungu, zitabweretsedwa ku Moyo, ndipo iko ndi Kuwala kwakukulu kuposa momwe kunaliri pa kucha kwa chirengedwe. Amen! Kuwala ku nyali, ku njira. Mai! O Mulungu! Kuwala, Mawu!

<sup>158</sup> Mu mdima monga ife tirimo lero, odzazidwa ndi tizikhulupiriro ndi zipembedzo, odzazidwa ndi zogirigisha ndi zotentheka, mitima yotseguka ku manda a mtundu uliwonse wa mzimu, umene umakhoza ngakhale kukana Mawu awa kukhala Choonadi, ndi kumati, “Masiku a zozizwitsa anatha. Kulibeko chinthu choterocho monga ubatizo wa Mzimu Woyera, kuyankhula ndi malirime, aneneri, ndi zina zotero. Iwo anafa, zaka zapitazo.”

<sup>159</sup> Ndiye nkumuwona Mulungu, mkatikati mwa mdima, mdima wa kachikhulupiriro, mdima wa zipembedzo, akutenga Mawu Ake ndi gulu la anthu amene ati akhulupirire Iwo, ndi kuwalitsa Kuwala Kwake ndi Moyo Wake. Ndi Kuwala kochuluka. Ndi Kuwala Kwamuyaya, kuposa momwe kunaliri pa kucha kwa chirengedwe. “Kuwale; ndipo kunali kuwala.” Ndithudi.

<sup>160</sup> Tsopano, Yesu sananene konse, tsopano, kuti Iye awabweretsa iwo ku Betelehemu. Yesu sananene konse kwa Agriki aja, pamene iwo anabwera, “Tsopano, mphindi chabe. Ngati inu mukufuna kuti muwone Izo, Ine ndikutengerani inu mmbuyo ku Betelehemu kumene Ine ndinabadwirako. Ndipo Ine ndikuuzani inu momwe izo zinachitikira kumbuyo uko.” Izo sizinali zimenezo.

<sup>161</sup> Iye anawalozero iwo ku malo a mtsogolo, ngati iwo amafuna kuti amudziwe Iye. “Ngati inu mukufuna kuti mundidziwe Ine,” mwa kuyankhula kwina, “Ine sindikutengerani inu mmbuyo ndi kukakuuzani inu za nthawi imene Ine ndinabadwa ku Betelehemu, ndi zonse za izo. Ine ndikulozerani inu ku malo amene Ine nditi ndikapachikidweko chifukwa cha inu. Ndipo mmenemo, ngati inu muti mudzapachikidwe ndi Ine, ndi kutenga mtanda wanu ndi kunditsatira Ine, inu mudzadziwa Yemwe Ine ndiri. Kupanda kutero, kuchokera pamenepo, inu simudzaphunzira izo kudzera mu zojambula zanu zakale. Inu simudzatero.”

<sup>162</sup> “Chabwino,” inu mukuti, “M’bale Branham, koma ife timaphunzira Izo kudzera mu luso la Baibulo.” Ayi. Ife sititero. Ngati ife tingaphunzire izo kudzera mu luso la Baibulo, ndiye nchifukwa chiyani Afarisi analibe Izo? Izo sizimaphunziridwa kudzera mu luso la Baibulo, chifukwa ilo liri ndi aluso ochuluka kwambiri amene akuyesetsa kuti ajambule izo. Koma Baibulo ndi lolondola, koma Mulungu ndiye Wojambulayo.

<sup>163</sup> Tizikhulupiriro lero timati, “Mujowine *ichi*. Muzinena matamando *awa*. Muzibwereza Kachikhulupiriro ka Atumwi. Mujowine mpingo wathu. Gwiranani chanza. Mubatizidwe, mu dzina la ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera.’” Ito ndi tizikhulupiriro ta chipembedzo. Kulondola. Wojambulayo sanajambule chithunzicho mwanjira imeneyo.

<sup>164</sup> Wojambulayo anajambula izo, mwakuti, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye amene amva

Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine ali nawo Moyo Wamuyaya. Ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Umo ndi momwe Wojambulayo anajambulira izo. Kotero pamene Mulungu akunyezimiritsa izo, iwe umadziwa kuti wakhudza kujambula koyenera. Kunja kwa zimenezo, ndiye kuti uli ndi chokopera chabodza. Amen. Mutenge chabodza chokopera chakale chija, cha mtundu wina wa kachikhulupiriro, ndipo mukachitaye chinthucho panja pa khomo, usikuuno. Ndipo mukatenge Kuwala kwa Uthenga wa Baibulo, ndipo mulole Wojambulayo akajambule Khristu mwa inu. Amen. Njira yake ndi imeneyo. Ndi zimenezotu.

<sup>165</sup> Ayi, Iye sanawatengere iwo kodyera ziweto. Iye sanawatengere iwo ku Khrisimasi.

<sup>166</sup> Yesaya anati, “Dzina Lake likanadzatchedwa . . .” Mu mutu womwewo, iye anati, “Dzina Lake lidzakhala . . .” Ayi, mutu wa 55 wa Yesaya. Anati, “Dzina Lake lidzatchedwa Wodabwitsa, Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu wamphamvu, Atate wosatha.” Amen.

<sup>167</sup> Ndikanakonda ndikanakhala ndi nthawi. Ine ndikuyenera kutero. Ine ndikufuna kuti ndidzatenge phunziro pa aliwonse a iwo: “Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu wamphamvu, Atate wosatha, ndi Wodabwitsa.”

<sup>168</sup> Tiyeni tingogunda lingaliro loti Wodabwitsa, kwa miniti, Wodabwitsa. Oh, Yesaya anati Iye anali Wodabwitsa. Tiyeni tiganizire za zinthu zina zimene Iye ananena, zimene zinamupanga Iye kukhala Wodabwitsa. Nchiyani chinamupangitsa Iye kukhala Wodabwitsa? Pamene Iye ananena ichi, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi,” Wodabwitsa.

<sup>169</sup> Ndiwuzeni ine Mfarisi amene akananena zimenezo. Ndiuzeni ine wansembe wamkulu amene akananena zimenezo, ndipo Mulungu nkudzaikira izo kumbuyo. Mukuona?

<sup>170</sup> Anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchitozo tsopano, musakhulupirire chirichonse chimene Ine ndikunena. Koma ngati Ine ndikulalikira izi, ndiye zikusonyeza kuti Mulungu anandituma Ine kuti ndizichita zimenezo.”

<sup>171</sup> Anati tsopano, ndipo Iye anati, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi.” Osati, “Ine ndi Atate Anga ndife atatu.” Yesu ananena. Tsopano, kachikhulupiriro kamati, “Ine ndi Atate Anga ndife atatu.” Koma Baibulo linati, ndipo Yesu anati, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi.” Izo ndi Zodabwitsa. Mukuona momwe Mulungu, “anapangidwira thupi”? Aleluya! Osati wachiwiri wina, kapena wachitatu, kapena munthu wachinayi; koma Mulungu Mwiniwake. Yesu ananena chomwecho. Mutsutsane ndi Iyeyo, osati ine. Ine ndikungonena zimene Iye ananena. “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi. Si Ine amene ndikuchita ntchitozi. Ndi Atate Anga. Iye akukhala mwa Ine. Ngati inu

simukundikhulupirira Ine; mukhulupirire Mawu, chifukwa Iye ndi Mawu. Ndipo Mawu asandulika thupi, ndipo ndi Ineyo. Pachiyambi panali Mawu.”

<sup>172</sup> Wolemba Uthenga yemwewo, Yohane, anati, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

<sup>173</sup> Izo zimamupanga Iye ndi Mulungu kukhala Munthu yemweyo; ngati Mulungu ali Mawu, ndipo Iye ndi Mawu. “Ine ndi Atate Anga ndi Mmodzi,” ndiye. Oh, zimenezo ndi Zodabwitsa! Inde, bwana.

<sup>174</sup> Pali zinthu zambiri zimene ife tingakhoze kunena pa zimenezo, Zodabwitsa, zinthu zimene Iye ananena!

<sup>175</sup> Chinthu china Iye anati, “Ine ndi Kuwala kwa dziko.” Ndiuzeni ine wansembe amene angakhoze kunena zimenezo. Ndiuzeni ine chipembedzo chimene chingakhoze kunena zimenezo. Ndiuzeni ine kachikhulupiro kamene kangakhoze kunena zimenezo. Izo ndi Zodabwitsa.

<sup>176</sup> “Ine ndi Choonadi.” Oh, mai! Tizikhulupiro tathu tiri mamailosi milioni kutalikirana ndi Choonadi. Kachikhulupiro sikangamupangitse Mulungu kuwonetseredwa. Kachikhulupiro sikangatero.

<sup>177</sup> Chimodzimodzi monga Eliya ananenera, pamwamba pa Phiri la Karimeli, “Ngati Mulungu ali Mulungu, muloleni Iye ayankhe.” Kachikhulupiro sikangachite zimenezo. Ayi, bwana.

<sup>178</sup> Koma Mulungu adzachita zimenezo. Kodi Mulungu ndi ndani? Mawu, Mawu owonetseredwa. Iye adzachita zimenezo.

<sup>179</sup> “Ine ndi Kuwala kwa dziko. Ine ndi Choonadi chimene chiri mdziko. Ine ndine Njira.” Palibe njira yina koma Iye. Ndizo zonse. Musadutsire mu kachikhulupiro. “Bwerani kwa Ine.” Mukuona? “Ine ndine Njira, Kuwala, Choonadi.” Zonsezo, Iye anali. Amenewo ndi mawu opambana amene Iye ananena. “Ine ndine Njira. Ine ndine Choonadi. Ine ndine Kuwala. Ine ndine—Ine ndine Woyamba; Ine ndine Wotsiriza. Ine ndine Chiyambi; Ine ndine Mapeto. Ine ndine Iye amene anali, amene ali, ndi amene adzabwera. Ine ndine Muzu ndi Mphukira ya Davide. Ine ndine Nyenyezi yaku Mmawa. Ine ndine Alfa mpaka Omega. Ine ndine Zonsezo. Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi. Iye akukhala mwa Ine. Ine ndine Iye. Iye ndi Ine.”

Iwo anati, “Iwe, pokhala Munthu, ukudzipanga wekha Mulungu?”

<sup>180</sup> Oh, monga Iye ananenera kwa Afarisi nthawi yina, “Inu mukulakwitsa, posawadziwa Mawu a Mulungu, ngakhalenso mphamvu ya Mulungu. Inu mukulakwitsa, posadziwa izo.” Ndithudi. Mawu odabwitsa! Zodabwitsa!

Tiyeni tiganizire za ntchito zodabwitsa, nthawi yina. Kodi Iye anachita chiyani?

<sup>181</sup> Kodi Iye anali chiyani? Yesaya anati iye akanadzakhala Wodabwitsa. Pamene iye anamutchula Iye maina onse amene iye akanatha, “Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu wamphamvu, Atate wosatha,” zonsezi, iye anati, “Iye ndi Wodabwitsa basi.” Mawu Odabwitsa!

<sup>182</sup> Tsopano ife tikuti tiyankhule za ntchito zodabwitsa, kwa miniti. Kodi Iye ankachita ntchito ziti zomwe zinali zodabwitsa?

<sup>183</sup> Tsiku lina kunali mwambo wa maliro umene unkabwera kuchokera ku Naini—Naini. Mzimayi wamasiye, ndi mwana wake wamwamuna yekhayo, atafa, atagona pa machira, atawumitsidwa, mtembo, wowumitsidwa, akupita kumanda kuti ukayikidwe. Iye anali atayenda njira yonse kuchokera ku Nazareti. Mapazi ake, atatupa, afumbi, wotopa, wofooka. Iye anamva kulira kumeneko. Iye anayang’ana. Akubwera kumusi pa msewu, apo panabwera mkazi wamasiye wamng’ono, akusisima. Mnyamata wake, mwana wake yekhayo, anagona pa machira amenewo, atafa.

<sup>184</sup> Zinachitika, kumeneko, pamene anadutsa kumene kunali Yesu. Imfa ndi Moyo sizingakhalire limodzi, inu mukudziwa; chimodzi chiyenera kuchokapo. Iye anati, “Ayimitseni onyamulawo.” Anapita kumeneko ndipo anakamukhudza mwanayo. Ndipo moyo umene—umene unali mwa mnyamatayo, umene unali utapita mwinamwake kwa masiku awiri, unabwereranso. Ndikutha kungowona chinsalu chokulungira mtembocho chikuyamba kusuntha, ndikuwona anthu akuyamba kuyang’ana. Ndipo mwamuna amene anali wakufa, anaimirira pa mapazi ake, anayenda pamenepo ndipo anakayika mikono yake mowakumbatira amayi ake, mwinamwake. Zimenezo ndizo ntchito za Mulungu. Wodabwitsa! Sichoncho izo? Ndithudi zinali.

<sup>185</sup> Ine ndikukhoza kumuwona Yairo, wansembe wamng’ono, anali munthu wabwino. Iye anamukhulupirira Yesu, koma iye ankayenera kuti azisunge zimenezo mwabata, pa chifukwa cha oyanjana naye ake.

<sup>186</sup> Alipo okhulupirira amseri ambiri lero ngati amenewo, amawopa kuti achotsedwa mu mpingo mwawo. Mukuona? Amantha, Mulungu sangathe kuwagwiritsa ntchito amenewo. Mulungu akufuna munthu amene angayime pamenepo. Ngati zingatengere imfa, asindikiza zimenezo. “Musamuwope iye amene amawononga thupi, koma Iye amene amawononga thupi ndi kutumiza moyo ku gehena.”

<sup>187</sup> Yairo. Ine ndikumuwona Iye akupita kunyumba kwa uyu—kwa mtumiki uyu. Analowa mmene wamng’ono, mwana yekhayo, wa usinkhu wa zaka thwelovu, mtsikana wamng’ono atagonekedwa atawuma, wakufa, atagonekedwa pa kama. Thupi

lake laling'ono, lopanda moyo linali litagonekedwa pamenepo. Manja ake aang'ono, otumbululuka. Zikhadabo zake zinali zitasanduka zoyera. Milomo yake inali itakokedwera pansi. Malungo anali atamupha iye, kapena chinachake. Maso ake aang'ono anali atalowa ndipo anatsekedwa, ndipo chinachake chinali pa iwo, mwina mwake. Tsitsi lake laling'ono linali litapesedwa. Panali maluwa ndi zinthu zitamuzungulira iye. Ndipo amayi ndi abambo ake, anali akufuula. Oyandikana nawo, akufuula. Mwana wake yekhayo anali atapita.

<sup>188</sup> Ine ndikumuwona Iye akulowa mchipinda chimenecho. Amen. Ndipo Iye anayang'ana mozungulira. Iye anawaona iwo onse. Ndipo iwo anayamba kumuseka Iye. Iye anawatulutsa iwo mchipindamo. Izo ndi Zodabwitsa. Mukuona? Munthu mmodzi akhoza kutenga ulamuliro pa gulu lonse. Nchifukwa chiyani iwo sananene chinachake? Iwo ankachita mantha kuti anene chinachake.

<sup>189</sup> Bwanji iwo sakuwatsutsa Mawuwa lero? Iwo akuwopa kuti anene zimenezo. Ndizo zonse.

<sup>190</sup> Anakalowa mchipinda chimenecho, anatenga dzanja laling'ono, loziziralo, ndipo anayankhula mu chinenero chosadziwika, cha kunja uko kwinakwake. Ndipo mzimu wa mwana ameneyo unabwereranso, ndipo iye anakhalanso moyo. Ntchito zodabwitsa! Inde, izo zinali. Izo zinali ntchito zodabwitsa, zinatsimikizira kuti Iye anali Wodabwitsa.

<sup>191</sup> Ine ndikhozanso kunena za Lazaro, pamene iwo anali atawumitsa kale thupi lake, masiku foro mmbuyo mwake, anayika zosanjikiza ndi zosanjikiza za zonunkhira pa iye, ndi kukulunga nsaluyo mozungulira ndi mozungulira mnyamata uyu. Ndipo apo iye anali, atagona mmanda, ndipo atavunda. Mphuno yake inali itagwera mkati. Milomo yake inagwera pa nkhope yake. Mphutsi za pakhungu zinali zitayamba kumudya iye. Ndipo moyo yake unali pa ulendo wa masiku foro, wa kwinakwake.

<sup>192</sup> Ine ndikumuwona Iye, mapewa Ake aang'ono, akugwa. Oh, mai! Dziko likananena kuti, "Tayang'anani pa zimenezo. Tayang'anani pa Munthu ameneyo. Tayang'anani pa Iye. Ndipo inu mukumutcha Iye, Mulungu. Ndi Uyo pamenepo, akupita uko ku manda, akulira misonzi yachivundi." Baibulo linati Iye analira. Misonzi ikutsikira pa tsaya Lake, akufwenthera, pamene Iye ankapita ku manda. Iye anali Munthu pamenepo.

Koma ine ndikumuwona Iye akuti, "Kankhani mwalawo." Amen. Amen.

<sup>193</sup> Iye anasintha chochitikacho. Lazaro, yemwe anali atafa kwa masiku foro, anayima pa mapazi ake ndipo anakhalanso moyo. Ine ndikukhoza kuwona zonunkhiritsazo zikuyamba kufinyika kudutsa pa mabulangete omwe iwo anamukulungiramo iye. Chiyani? Moyo unali utabweramo kachiwiri. Kununkhako

kunali kutachokapo. Mnofu watsopano unali utabwerapo. Mzimu, umene unali masiku foro kwinakwakenso, unabwerera mu thupi lake, ndipo munthuyo anayima pa mapazi ake. Kukamba za kukhala Wodabwitsa, Wauphundu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu wamphamvu, pamenepo Iye anali. Ndithudi, Iye anali. Chabwino.

<sup>194</sup> Ife tikumupeza mkazi pa chitsime, pamene Iye anayima ndi kuyankhula ndi iye kwa maminiti pang'ono, ndi kumuuzza iye kuti anali ndi amuna faivi pa nthawi imeneyo. Iye anati, "Bwana, Inu mukuyenera kukhala mneneri. Ife tikudziwa kuti, pamene Mesiya adzabwera, chimenecho chidzakhala chizindikiro Chake."

<sup>195</sup> Iye anati, "Ine ndine Iye amene akuyankhula ndi iwe." Zodabwitsa! Sichoncho izo? Zodabwitsa!

<sup>196</sup> Usiku wina nyanja inali ikubangula. Iye anali akugona, chifukwa chotopa, basi monga munthu. Iye anali akugona, chifukwa chotopa. Adierekezi anali atalumbirira kuti iwo akanati amumize Iye usiku umenewo. Ndipo iwo ankaganiza kuti anali pafupi kumugwira Iye, pamene matanga anali ataphwasuka, nkhami zitathyoka, bwatolo linali litalowa madzi ndipo linali likudzaza. Iwo anathamangira mmbuyo, ophunzirawo anatero, anati, "Kodi Inu simukusamala kuti ife tikuwonongeka?"

<sup>197</sup> Ndipo Iye anadzuka, ndipo anapukuta tulo mmaso Ake. Anati, "Oh, inu a chikhulupiriro chochepe, Ine ndikhala ndi inu motalika bwanji?"

<sup>198</sup> "Kodi Inu muchita chiyani tsopano? Kodi Inu muchita chiyani kunja kuno pa nyanja ya mkuntho iyi pamene uyu, Galileya wamkulu uyu, akupita pansi pa funde lirilonse? Kodi Inu muchita chiyani, pamene mdierekezi wakhala kutsidya kwa phiri ilo kutaliko, akunong'oneza mafunde amenewo pansi monga choncho, akuponyera zimenezo?" Wotopa, inu mukudziwa. Inu mukudziwa, Iye kumusi uko. "Izo zikugwedeza madziwo, kwa sarte-kapena mapazi forte kukwera mmwamba. Kodi Inu muchita chiyani?"

<sup>199</sup> Anati, "Kodi Ine ndikhala ndi inu motalika chotani?" Anayika phazi Lake m'mphepete mwa bwatolo ndipo anati, "Mtendere, ukhalebe." Ndipo mphepozo zinasiya. Mwa kuyankhula kwina, Iye anati, "Mphepo, tseka kamwa yako. Mafunde, bwerera kumusi kumene umakhala." Panalibe ngakhale funde pamadzi. Anayima pamenepo ndi kumayang'ana pozungulira.

<sup>200</sup> Anabwerera mmbuyo, ndi gulu lodabwa la atumwi litayima pamenepo. Anakagonanso pansi kachiwiri, ndipo anakapitiriza tulo Take.

<sup>201</sup> Iwo anati, "Ndi Munthu wa mtundu wanji uyu?" Wodabwitsa. Amen. Wodabwitsa.

<sup>202</sup> Kodi inu simukukhulupirira kuti Iye anali Wodabwitsa? Ndithudi, Iye anali Wodabwitsa. Inde, bwana. Pamene Munthu ameneyo Mwiniwake anachoka Kumwamba, pamene dongosolo lonse la zammwamba linali korona Wake, nyenyezi billioni zirizonse zimene zinapachikika mdziko lapansi, nyenyezi iliyonse mamailosi mamillioni amenewo kupitirira, pamene izo ziyang'ana kudzera mgalasi limenelo, kutali uko ku Phiri la Palomar, ndipo amatha kuwona zaka handiredi ndi twente millioni za danga la kuwala, ndipo mabillioni onsewo ndi matrillioni a nyenyezi zinali mu korona Wake, ndipo Iye anazisiya zimenezo, kuti adzavale chisoti cha minga. Ndani akanachita zimenezo? Wodabwitsa. Oh, mai!

<sup>203</sup> *Wamuyaya* unali Mkanjo Wake, Iye anavekedwa ndi Moyo Wamuyaya. Iye sanakhalepo konse ndi chiyambi, Iye sanayambire konse ku Betelehemu, inu mukudziwa, monga momwe anthu amayesetsera kuganiza kuti Iye anatero, Iye analibe chiyambi. Amen. Anavekedwa ndi Moyo Wamuyaya, ndipo anawukankhira Iwo kumbali, kuti adzatenge mkanjo wakale wakuda wa imfa chifukwa cha inu ndi ine. Wodabwitsa. Uh-huh.

<sup>204</sup> Kumwamba kunali Nyumba Yake Yachifumu. Kumwamba konse kunali kwa Iye, Imeneyo inali Nyumba Yake Yachifumu. Palibe chimene chikanakhoza kuwala konse ndi Iye. Ndipo Iye anabwera ku dziko lapansi, ndipo mpaka anati, “Nkhandwe ziri ndi mayenje, mbalame ziri ndi zisa, koma ine ndiribe ngakhale malo oti nkuyikapo mutu Wanga.” Izo ndi Wodabwitsa. Kodi inu simukuganiza chomwecho?

<sup>205</sup> Abwenzi, pali zolemba zambiri zimene ine ndazilemba apa. Koma ine mwinamwake ndiribe nthawi yoti ndizitenge izo. Ine ndifulumira mwamsanga.

<sup>206</sup> Ameneyo ndi Yesu amene inu mukuyenera kumuwona. Osati Yesu wa chipembedzo amene iwo amamukamba; osati Yesu wa tizikhulupiriro; osati Yesu wa mtundu wina wa nthano ya Khristimasi; osati Yesu wa Isitara yina ya kalulu; koma Yesu wa Kalvare, Yesu Amene anayika pambali chirichonse, Amene aneneri ankamukamba.

<sup>207</sup> Ife tikanakhoza kumapitirira apa, “Atate Wodabwitsa, Wodabwitsa, Atate Wodabwitsa, Wauphungu Wodabwitsa, Kalonga wa Mtendere Wodabwitsa, Mulungu wamphamvu Wodabwitsa.” Ife tikungopitirirabe, kumapitirira, kumapitirira. Mukuona? Koma kuyika pambali, ife tikunena ichi, “Ife tikuyenera kuwona, ngati inu...Uyo ndi Yesu amene ife tikuyenera kumuwona, kuti tikhale ndi Moyo Wake Wamuyaya.”

<sup>208</sup> Inu simungawupeze iwo mu kachikhulupiriro. Inu simungawupeze iwo mu kujowina mpingo. Inu simungawupeze iwo mu mtundu wina wa nthano zomwe inu mumawuzidwa

za, Santa Claus. Santa Claus alibe Moyo Wamuyaya. Ayi. Kachikhulupiriro kalibe Moyo Wamuyaya.

<sup>209</sup> Osati kuwadziwa Mawu Ake, ngakhale kukupatsani inu; kuwadziwa Iwo, Iwo samakupatsani inu Moyo Wamuyaya. “Kumudziwa Iye,” Baibulo linati, “kumudziwa Iye, ndi Moyo Wamuyaya.” Osati kudziwa Mawu Ake. Kumudziwa Iye!

<sup>210</sup> Agriki ankafuna kuti amuwone Iye. Iwo ankafuna kudziwa umunthu Wake. “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.”

<sup>211</sup> Tsopano, inu simumawona ndi maso anu. Inu mumawona ndi mtima wanu. Mukuona? Inu mumayang’ana ndi maso anu. Inu mumamvetsa ndi mtima wanu. *Kuwona* ndi “kumvetsa.” Inu mumayang’ana pa chinachake, nkuti, “Ine sindikuchiwona icho.” Koma, inu mumakhala mukuyang’ana pa icho. Koma, inu mumatanthauza, kuti “simukumvetsa” icho.

<sup>212</sup> Agriki ankafuna kuti amudziwe Yesu, ndipo Iye anawapatsa iwo njira yomudziwira Iye. Kumudziwa Iye! Osati kudziwa kachikhulupiriro Kake, osati kudziwa Mawu Ake, osati kudziwa zozizwitsa Zake, koma kumudziwa Iye! Ndipo njira yokhayo imene inu mumapezera izo, ndi pa mtanda, osati chikuta. Ayi. Ndi ku mtanda kumene ine ndimakamuwonako. Iye anawalozera iwo ku mtanda, osati ku...Osati ku kachikhulupiriro kenakake, kapena—kapena osati modyera ziweto mwinamwake, kapena mtundu wina wa zipembedzo, koma ku mtanda.

<sup>213</sup> Ndipo tsopano izo ziri chimodzimodzi lero, wophunzira weniweni, ndipo ngati inu munayamba mwafika konse kwa Yesu. Iye sadzati konse, “Yesu anandiuza ine kuti ndipite ndikajowine mpingo *wakuti-ndi-wakuti*.” Iye sanachitepo konse zimenezo. Iye sangachite zimenezo lero. Ayi.

<sup>214</sup> Inu mukafuna kuti mumuwone Iye, Iye adzakulozerani inu ku mtanda. Pitani kumeneko ndipo mukafe, mukatero inu mudzamudziwa Iye, ngati mukufuna kuti mumudziwe Iye.

<sup>215</sup> Palibe nthawi imodzi imene Iye anamulozerapo munthu aliyense ku kachikhulupiriro kalikonse, chipembedzo chirichonse, kapena ku kubadwa Kwake, kapena ngakhale ku Khristimasi. Palibe nthawi imodzi imene Iye anayamba wachitapo izo konse. Ine ndikanakhoza kukhalitsa pa zimenezo kwa kanthawi, koma ine—ine sinditero. Komabe, ngati izo siziri zofunikira, ngati Yesu...Inu simungakhoze kuzipeza izo kulikonse mu Baibulo, pamene Iye anayamba wamulozerapo aliyense kulikonse, kuti amudziwe Iye, koma ku mtanda. Uko nkulondola. Ndipo uko ndi kudzipachika wekha kwa iwemwini. “Pokhapokha munthu atabadwa mwatsopano.” Ndiyeno, ngati modyera ziwetomo, Santa Claus... .

<sup>216</sup> Yesu sanalembepo konse kachikhulupiriro. Iye sanadzozeapo konse chipembedzo. Ndiyeno nchifukwa chiyani ife timapanga zochuluka kwambiri za izo, ndipo ngakhale kuyika udindo

uliwonse pa izo? Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu zimenezo; Khristimasi, tsopano. Nchifukwa chiyani ndiye mipingo yathu imakhazikika kwambiri pa zimenezo, kuti, “Iwe ukuyenera kukhala wa mpingo *uwu*. Iwe ukuyenera kunena kachikhulupiriro *aka*. Iwe ukuyenera kuchita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*”? Nchifukwa chiyani ife timakhazikika kwambiri pa zimenezo, ngati izo sizofunikira? Zimawonetsera kuti tiri ndi ophunzira a mtundu wosiyana ndi amene tinkakhala nawo poyamba. Iwo amafuna kuti akubweretseni inu ku mpingo wawo, ku chipembedzo chawo, kapena ku kachikhulupiriro kawo, ndipo osati kwa Khristu.

<sup>217</sup> Anthu lero, ngati iwo afunsidwa, “Kodi ndinu wokhulupirira?” Ine ndafunsapo izi, nthawi zambiri. “Kodi ndinu wokhulupirira?”

<sup>218</sup> Iwo amati, “Oh, ndine wa Baptisti. Ndine wa Methodisti.” Chabwino, izo zimasonyeza kuti sindinu wokhulupirira pamenepo. Mukuona? Uko nkulondola. “Baptisti, Pres-...” Koma inu mumati, “Ndine wa Pentekoste.” Izo ziribe chinthu chimodzi chochita ndi zimenezo. Ayi, bwana. Wokhulupirira ndi cholengedwa chatsopano. Koma uko ndi kumene iwo azifikitsa izo, lero. Mukuona? Nchifukwa chiyani iwo amachita zimenezo? Nchiyani chimawapangitsa anthu kumanena zimenezo?

<sup>219</sup> Usiku wina, ine ndinali mchipatala. Ine ndinali woti ndikamupempherere mkazi wamng’ono amene ankadwala. Iye anachiritsidwa. Ndipo ine ndinati... Panali mwamuna ndi amayi ake atakhala pamenepo. Ine ndikuganiza kuti anali amayi ake. Ndipo iwo ankawoneka ngati amayi ake. Ndipo ine ndinali kuyankhula ndi donayo. Ine ndinati, “Ife tikhala ndi pemphero tsopano.”

Ndipo ine ndinatembenuka, “Inu mudandaula ngati ife tingapemphere?”

Iye anati, “Kokani katani imeneyo.”

Ine ndinati, “Chabwino, ine ndinangofunsa ngati inu mungadandaule ife titati tipemphere.”

Iye anati, “Ndife Amethodisti. Kokani katani imeneyo.”

<sup>220</sup> Ine ndinati, “Ndiye ichi chingakuwopsyezeni inu mpaka ku imfa. Ine kulibwino ndikoke kataniyo ndiye, mwaona.” Ine ndinati, “Ngati mwangokhala wa Methodisti, inu sindinu Mkristu. Chotero ine basi...” Eya.

<sup>221</sup> Nchifukwa chiyani iwo amanena zimenezo? Wophunzira wina wabodza anangowatengera iwo kutali chomwecho. Ndizo zonse zimene iwo amazidziwa, wophunzira wina wophunzitsidwa molakwika. Ophunzira a Yesu anawatengera iwo kwa Yesu. Wophunzira wa Methodisti amawatengera iwo ku Methodisti. Wabaptisti amawatengera iwo kwa Abaptisti. Ndipo Wachipentekoste amawatengera iwo kwa Achipentekoste. Koma

wophunzira wa Khristu amawatengera iwo kwa Khristu, ndipo Khristu amawatengera iwo ku Kalvare. Ichu ndicho chinthu chenichenicho. Inde, bwana. Inde, bwana.

<sup>222</sup> Uwo ndi utali wa momwe iwo anawabweretsera. Iwo anangobweretsedwa motalika chomwecho. Mukuona? Ngati iwo—iwo amati, chabwino, “Wa Baptisti, kapena wa Methodist, kapena wa Presbateria, kapena *chiyani*,” uwo ndi utali womwe iwo anabweretsedwera, “Katolika,” chirichonse chimene icho chiri. Uwo ndi utali womwe iwo anabweretsedwera, kotero ndizo zonse zomwe iwo amazidziwa.

<sup>223</sup> Koma, tikuthokoza Mulungu, ophunzira awa ankamudziwa Yesu. Kotero iwo anamutengera iye kwa... Iwo anawatengera Agriki awa kumene iwo ankadziwa kuti kunali Choonadi. Ndipo wophunzira weniweni wa Khristu, amene anayamba wamupezapo Khristu, amamutengera—wofunafunayo molunjika kwa Yesu. Ndipo Yesu amawalozero iwo ku Kalvare, kumene iwo amakafa ndi Iye ndipo amabadwa mwatsopano, mwatsopano. Oh, mai! Uwo ndi mtunda umene iwo amapita.

<sup>224</sup> Koma, “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.” Limenelo linali funsolo. “Ife sitikufuna kuwona kachikhulupiriro. Ife sitikufuna kuwona Amethodisti. Ife sitikufuna kuwona Abaptisti. Ife sitikufuna kuwona chirichonse cha izi. Ife tikufuna timuwone Yesu.” Koma vuto ndi chiyani?

<sup>225</sup> Ine ndikungoyenera kuti nditseke, abale anga. Mvetserani mwatcheru tsopano, ndemanga pang’ono chabe apa ife tisanatseke. Chiyani? Ine ndikufuna kuti ndichipange ichi kumveka tsopano, ngati ine ndingathe, kukhomerera chinthucho pansu.

<sup>226</sup> Agriki ankafuna kuti amuwone Yesu. Iye sanamupeze Iye mu Khrisimasi. Sanamupeze Iye mu bungwe linalake. Sanamupeze Iye mu kachikhulupiriro kenakake. Iye sanawalozero iwo kwa zoterozo. Kodi inu mwamvetsa zimenezo bwinobwino? Koma Iye anawalozero iwo ku mtanda, kuti akafe, kuti akafe. Wophunzira weniweni amati, “Inu mukuyenera kuti mufe.” Ine ndingadziwe bwanji pamene ine ndiri wakufa? Pamene inu muzindikira Mawu onsewa kuti ndi Choonadi, kenako Mawu amayamba kukhala moyo mwa inu.

<sup>227</sup> “Chabwino,” inu mukuti, “koma mpingo wathu umaphunzitsa...” Ine sindikusamala zomwe mpingo wanu umaphunzitsa. Ndi zomwe Baibulo limanena. Kumene inu mukupitako, mpingo wina umaphunzitsa chinachake chosiyana. Koma Baibulo ili limaphunzitsa zofanana.

<sup>228</sup> Ndipo Yesu anati, “Pamene inu muwalandira Mawu awa, Mawu awa adzawonetseredwa mwa inu. Iwo adzachita chinthu chomwecho chimene Iwo amanena kuti Iwo adzachita mwa inu.”

“Oh,” iwo amati, “masiku a zozizwitsa anapita.”

<sup>229</sup> Ndipo Baibulo linati, “Yesu, ali yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse.” Inu mukwanitsa bwanji kuzipanga zimenezo kuti zikumane pamene Yesu anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine,” kulikonseko, nthawi iliyonse?

<sup>230</sup> Marko 16 anati, “Pitani inu ku dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.” Mpaka kuti? “Ku dziko lonse lapansi.” Sunafike ngakhale kumeneko panobe, “Cholengedwa chirichonse.” “Iye amene akhulupirira ndi kubatizidwa adzapulumutsidwa. Iye amene sakhulupirira adzalangidwa. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ndi zimenezotu. Mawu adzasandulika Kuwala. Iwo adzaziwalitsa Okha.

<sup>231</sup> Osati ngati inu mupita ku chikuta ndi kukati, “Mwana wamng’ono anabadwira kuno, zaka zambiri zapitazo.” Zamkutu. Mitundu yonse ya tizikhulupiriro ndi nthano zonedwa za zimenezo. Ife tikudziwa kuti Yesu ankadziwa kuti chinthu chonsecho chikanadzawonongeka, kusokonezedwa chonsecho.

Koma pali Chinthu chimodzi chimene sichiri chosokonezeka, ndicho Mzimu Woyera.

<sup>232</sup> “Oh,” mmodzi wa iwo amati, “Iye anabadwira pomwe *pano*. Ife tinamangapo tchalitchi pamenepo.” Winayo anati, “Iye anabadwira cha *kuno*.”

<sup>233</sup> Monga, inu mukudziwa kuti ndi misomali ingati imene iwo ali nayo, tikhoza kutsimikizira izo, misomali yapachiyambi imene inali pa mtanda? Naintini. Munthu aliyense atanyamula msomali. “Uwu, *ife* tiri nawo. Aleluya, *ife* tiri nawo iwo.”

Iwo angokhala ndi mafupa ena akufa a china. “*Ife* tiri nacho icho. *Ife* tiri nacho icho.”

<sup>234</sup> “*Awa* ndi malo amene Iye anabadwirapo.” Winayo amati, “*Awa* ndi malo amene Iye anabadwirapo.” Uyu akuti, “*Awa* ndi malo amene Iye anabadwirapo.” Kodi izo zimapanga kusi yana kotani?

<sup>235</sup> *Apa* ndi pamene Iye anabadwirapo, mu mtima. Eya. Pamene ine ndinafa, Iye anabadwira *munu*. Ine ndinabadwa mwatsopano, mwa Iye, mwatsopano. Ndi zimenezotu.

“Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.” Chabwino.

<sup>236</sup> Chabwino, vuto ndi chiyani? Iye watayika kachiwiri. Anthu amutaya Iye. Uko nkulondola. Koma Iye watayika kachiwiri, m’magulu aakulu, magulu a tizikhulupiriro. Inu mukukumbukira nthawi ina Iye anasowa, kwa makolo Ake? Iye wasowa kachiwiri. Iye anasowa.

<sup>237</sup> Anapita uko m’misewu iyi, monga zimakhala zikukhalira mmasiku angapo apitawa, kuyang’ana mmaunyinji amisala, akukankha ndi kulaisha, ndi kumwa, ndi kutukwana, ndi

kutemberera. “Mabelu, mabelu.” Khristu wasowa. Iye sanasowe. Anthu amutaya Iye.

<sup>238</sup> Kodi iwo anakamupeza kuti Iye? Kumene iwo anamutaya Iye. Ndi kumene ife titi tikamupeze Iye.

<sup>239</sup> Koma Iye wasowa, mu tizikhulupiriro tawo ndi mmagulu awo. Iye wawasowa. Khristu wasowa, mu gulu la zamalonda. Gulu la zamalonda likuti, “Ife tikuyenera kuti tikondwerere Khristumasi.”

<sup>240</sup> Dona ananena tsiku lina, atayima pamenepo, pamene mkazanga ndi ine tinali titayima pamenepo. Anati, “Ine ndawagulira abambo anga botolo la kachasu.”

<sup>241</sup> Winayo anati, “Chabwino, ine ndigula... ine ndikuuzani inu chimene ine nditi ndiwagulire adadi. Ine ndiwagulira iwo makhadi ndi tchipisi. Tikasewera njuga, mukuwona, kukondwerera Khristumasi.”

<sup>242</sup> Ena anati, “Ine ndangogula katonu ya ndudu ya amayi. Inu muwagulira iwo chiyani?” Huh! Huh!

<sup>243</sup> O Mulungu! Iye wasowa. Iwo anamutaya Iye, mu Khristumasi. Iwo anamutaya Iye, mu Isitara. Kalulu, kapena chipewa chatsopano; osati chiwukitsiro, osati kubadwa kwa Khristu.

<sup>244</sup> Iwo anamutaya Iye, mu tizikhulupiriro tawo, pamene iwo anapanga milungu itatu kuchokera mwa Iye, anamuduladula Iye mzdutswa ndi kupanga mafano, mmalo modziwa yemwe Iye ali. “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi.” Inu munamutaya Iye.

<sup>245</sup> Iye wasowa, mu gulu lawo lachipembedzo. Kodi gulu la chipembedzo linachita motani? Iye wasowa, ku mpingo Wake, mu Laodikaya. Mpingo wotsiriza, m’badwo wa mpingo, iwo anati Iye anali kunja kwa mpingo, “akugogoda,” akuyesetsa kuti alowe mkati. Mawonekedwe omvetsa chisoni kwambiri mu Baibulo lonse, ndi chikhalidwe cha mpingo m’masiku otsiriza Iye asanabwere. Palibe m’badwo wa mpingo wina umene unayamba wamuyikapo Iye kunja. Iwo sankadziwa kusiyana kulikonse. Tsopano pamene iwo akudziwa kwenikweni m’phamvu yona ya Mzimu Woyera, iwo anamukankhira Iye kunja kwa malowo, kunja, akugogoda pa chitseko. “Taonani, Ine ndayima pakhomu ndipo ndikugogoda.” Ndithudi.

Iwo anamutaya Iye, m’magulu awo azamalonda.

<sup>246</sup> Iwo anamutaya Iye, mmagulu awo achipembedzo. Uko nkulondola. Iwo anapanga tizikhulupiriro kuchokera mwa izo. Iwo anapanga zipembedzo kuchokera mwa izo. Iwo anazitaya izo. Iwo anatenga—iwo anatenga mwambo mmalo mwa Baibulo. Iwo anatenga gulu la malingaliro a anthu mmalo mwa chimene Mulungu ananena. Iwo anati, “Lembani dzina lanu pa bukhu. Gwiranani chanza. Ndizo zonse zimene inu mukuyenera kuchita. Mubatzidwe, ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.’” Chinthu chonsecho ndi chabodza. Uko nkulondola.

<sup>247</sup> Apo ndi pamene gulu la mpingo linamutayira Iye, pamene iwo anamutaya Iye. Bwanji? Osati mnyumba zawo za tchalitchi, osati mu zawo zomwe inu mumazitcha izo, lawo—gulu lawo la anthu. Koma iwo anamutaya Iye pamene iwo anawasiya Mawu. “Ngati izo... Ngati inu mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga nkukhala mwa inu, pemphani chimene inu mukuchifuna. Ichochidzaperekedwa kwa inu. Ichochidzachitidwa kwa inu, ngati inu mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga nkukhala mwa inu,” chifukwa ndi Mulungu, atasandulika thupi kachiwiri. Mukuona? “Inu mukakhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga nkukhala mwa inu, ndiye mungopempha chimene inu mukufuna. Ichochidzachitidwa kwa inu.” Ndi zimenezotu.

<sup>248</sup> Koma, lero, iwo sakukhalamo. Iwo ali, lero, Amethodisti, mawa Abaptisti, tsiku lotsatira Apresbateria, sanafike kulikonse panobe.

<sup>249</sup> “Ngati Mawu Anga akhala mwa inu! Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Aleluya!

<sup>250</sup> M’bale Neville, izo ndi zoona kwambiri.

Mawu atawumbidwa mu thupi lanu, akuyankhula kudzera mwa inu.

<sup>251</sup> Apentekoste anamutaya Iye. Oh, inde. Iwo anali ndi Iye, zaka zingapo zapitazo, koma iwo anamutaya Iye. Kodi iwo anachita motani izo? Powona yemwe akanakhoza kumanga nyumba yayikulu kwambiri, uh-huh, amene akanakhoza kukhala ndi tchalitchi chachikulu kwambiri, kwaya yophunzitsidwa bwino kwambiri.

<sup>252</sup> Ngati pali chirichonse chimene ine sindimachikonda, ndi liwu lophunzitsidwa mowonjeza, limene amayima ndi kumayimba ngati kuti iwo ali ndi vuto loliralira, amvekere “whii,” kugwira mpweya wawo mpaka kuda pa nkhope. Iwo sakuyimba. Iwo akungopanga phokoso.

<sup>253</sup> Koma chimene ine ndimachikonda ndi kayimbidwe kabwino, kachikale, komveka mu mtima, kachipentekoste, ka munthu wobadwa mwatsopano, kochokera mu mtima mwawo. Ngati iwo sangakhoze kunyamula kayimbidwe mu chidebe, iwo amakhalabe ndi Mzimu mmenemo. Inu mumakhoza kuwumverera Iwo ukung’amba kudutsa mwa iwe. Aleluya! Ine ndimazikonda zimenezo. Ine ndimazikonda zimenezo ndi zotsatira zake, Mzimu Woyera ukudalitsa izo, inu mukudziwa. Ine ndimazikonda zimenezo. Izo ndi zenizeni basi, kwa ine. Eya.

<sup>254</sup> Koma iwo anamutaya Iye. Makwaya ophunzitsidwa bwino ndi alaliki ophunzitsidwa bwino. Eya. Oh, mai! Mitundu yonse ya tsitsi lopiringizika, inu mukudziwa, ndi kumaweramitsa mutu wawo chaku mbali *iyi*, kumajambula chithunzi chawo. Ndipo, oh, eya, ophunzitsidwa-bwino. Iwo ndithudi ali. Amenewo ndi ophunzitsidwa-bwino.

<sup>255</sup> Ma Sande sukulu aakulu, ndithudi, mpingo uliwonse ukuyesetsa kuti upose wina, mu Sande sukulu. Ndipo Sande sukulu simayankhulidwa nkomwe, mu Baibulo. Chimenecho ndi chiphunzitso cha Methodist. Iyo poyamba inkatchedwa “sukulu ya ana osauka.” Aliyense tsopano amapita ku Sande sukulu, amene sangakhale ku tchalitchi, chifukwa iwo anatenga chinachake pambali pa chimene Mulungu ananena. Kulondola.

<sup>256</sup> Kumbukirani, ine sindinanenepo konse kuti ndinalalikirapo chirichonse pansi pa kud zodza, m'moyo wanga, chimene ine ndinkayenera kuchibweza, monga momwe ine ndinachitira ndi maguwa, tsiku lina, ndi zinthu, inu mukudziwa, *Mbewu Ya Serpenti*, kapena chirichonse cha izo. Mulole winawake abwere ndi kudzazing'amba izo ndi Mawu a Mulungu. Ayi.

<sup>257</sup> Apo ndi pamene iwo anamutaya Iye; Sande sukulu yaikulu, kapena hema yaikulu kwambiri imene ilipo, gulu lovala bwino kwambiri mu mzinda. Ameneyo ndi Pentekoste. “Bwanji, ife ndi a mpingo woyamba. Gulu labwino kwambiri mu mzindawu limapita kumeneko.” Madikoni, okwatira katatu kapena kanayi, madikoni pa bodi, mwinamwake abusa, nawonso. Mitundu yonse ya zamkutu m'mipingo lero. Mukuona? Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anamutaya Yesu.

<sup>258</sup> “Chabwino, inu mukudziwa, chipembedzo chathu ndi chachikulu kwambiri mu Pentekoste. Amuna athu ndi amuna ophunzitsidwa bwino kwambiri amene alipo mmenemo.” Iwo akhoza kukhala zonsezo. Ine sindikukana zimenezo. Zimenezo zimapita ku malozi ndi kumadera a zafioloje.

<sup>259</sup> Koma ine ndikufuna kumudziwa munthu amene amamudziwa Yesu, amene anamuwonapo Iye ndipo anabadwa mwatsopano, ndipo Mawu akudzinyezimiritsa Okha mu mawu ake. Inu mukhoza kuwona kuti Iwo si ake. Ndipo iye wadzipereka yekha kwathunthu mpaka zikumakhala kuti Khristu akuyankhula kudzera mwa iye. Ndi zimenezotu. Uko nkulondola. Ndipo zizindikiro ndi zodabwitsa zimatsatira Mawu amenewo, chifukwa Iwo ndi Mawu a Mulungu.

<sup>260</sup> Koma ngati Mawu a Mulungu anena chinthu chinachake, ndipo gulu *ili* nkudzati, “Oh, ayi. Ayi, ayi. Bungwe lathu litikankhira ife kunja ngati ife tikhulupirire Iwo.” Ndiye iye watha, pomwepo. Iye wadzidula yekha, pomwepo. Ndizo zonse. Inu mukhoza kupanga chinachake mwa kudzipangitsa. Inu mukhoza kuchita mtundu wina wachinyengo, kulingalira *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*, koma chinthu, chenichenicho sichiri pamenepo. Inde, bwana. Oh, ndithudi.

<sup>261</sup> Mipingo, mipingo ikumusinthanitsa Khristu ndi dziko ndi tizikhulupiriro. Mpingo uli pa dongosolo losinthanitsa. Oh, iwo ndithudi akufuna ku—kusinthanitsa. Inde, bwana. Iwo amapita ndipo iwo amakasinthanitsa. Iwo akufuna a—iwo akufuna dongosolo losinthanitsa. Iwo akufuna kusinthanitsa chimene

Mulungu akunena, ndi chimene chipembedzo chikunena. Iwo akufuna kusinthanitsa chimene Mulungu akunena, ndi “muzimutsatira m’busa.” Iwo akufuna kusinthanitsa chimene Mulungu akunena, ndi “zitsatirani bungwe.” Iwo akusinthanitsa.

<sup>262</sup> Kodi inu mukudziwa chiyani? Anthu akugula. Oh, pali zamalonda zazikulu zimene zikuchitika tsopano. Ndi Khrisimasi ina, zachinyengo chabe, zongopanga.

<sup>263</sup> Ife tinali ndi nthawi yowonjezera pang’ono, ine ndidzabwereranso pa phunziro ili kachiwiri tsiku lina. Ndikudutsa zochuluka kwambiri apa, zimene Mzimu Woyera unandipatsa ine kanthawi kapitako. Mukuona?

<sup>264</sup> Pamene mpingo ukusinthanitsa, mpingo ukugula, anthu akutero, otchedwa mpingo. Inde, bwana. Iwo akusinthanitsana. Iwo ndithudi akugula ndi kusinthanitsana. Iwo akugula chiyani? Mpingo waukulu kwambiri, gulu lovala bwino kwambiri, chipembedzo chachikulu kwambiri. Ndipo anthu... ine ndinena chinachake. Anthu akuyesetsa kuti apeze, ngakhale Achipentekoste, akazi Achipentekoste akuyesetsa kuti apeze malo omwe angamawalole iwo kuti azipitirira ndi zinthu zochuluka za mdziko: akabudula, tsitsi lodula, penti. Iwo akugula.

<sup>265</sup> “Mulungu adalitsike, ndine wa Chipentekoste. Aleluya! Ndine wa *ichi*. Ndipo, oh, abusa athu samakhulupirira...”

<sup>266</sup> Inu mwaona, inu mukuwagulira iwo amene ati adzawalole iwo kukhala mwauve kwambiri, (Mulungu atichitire chifundo), iye amene adzawalole iwo kukhala monyansa kwambiri ndi mofanana kwambiri ndi dziko, momwe iwo angathere. Iwo akugula kuchokera kumalo kupita kumalo, kumukana Khristu. Izo zikhoza kupera monga chirichonse. Izo ndi zoti zizichita zimenezo. Anthu akugula. Iwo akugula za pa Khrisimasi komwe angakapezeko mitengo yonenerereka. Osaka-konenerereka!

<sup>267</sup> “Chabwino, ndine wa Pentekoste, nanenso. Chabwino, ife tiribe Zinthu zakale za malingaliro-owonda zimenezo.” Koma Baibulo limanena chomwecho.

Ngati iye ali wophunzira woona wa Khristu, iye adzakutogolerani inu ku mtanda.

<sup>268</sup> “Oh, M’bale Branham, ine ndinapita uko ndipo ndinakayankhula mmalirime.” Zimenezo sizitanthauza kanthu. Mphongolo inachita zimenezo, tsiku lina. Inde, bwana. Ndizo eya...

<sup>269</sup> Ine sindikutanthauza kuwanyoza Mawu oyera a Mulungu. Ine ndimakhulupirira mu kuyankhula mmalirime.

<sup>270</sup> Koma ziwanda zimayankhula ndi malirime. Anthu akhoza kuyankhula mmalirime ndi kumakhala moyo wa mtundu

uliwonse. Koma, ine ndikutanthauza, a—mdierekezi ali ndi—chokopera cha chirichonse chimene Mulungu anachita.

<sup>271</sup> Ndipo iye akhoza kukopera chirichonse kupatula Kubadwa kwenikweni kwa Khristu, ndipo iye sangathe kuchita zimenezo. Chifukwa, iwe ukuyenera kufa, choyamba, kenako Mawu amakudzutsa iwe. Iwe umadziwa bwanji kuti uli moyo? Pamene Mawu amenewo, Mawu aliwonse a Iwo, asandulika thupi mwa iwe. Chirichonse chimene Baibulo limanena, iwe umanena chinthu chomwecho, ndipo icho chimadzachitika ndendende basi monga Iye ananenera icho. Ndi pamene izo zimakhala, inde, pamene iwe, pamene mzimu wako ugwirizana ndi Iye. Iye ndi Mawu. Pamene mzimu wako ugwirizana ndi zomwe Iye ananena, ndipo Mzimuwo umadzipangitsa Wokha kuwonekera kupyolera mu Mawu Ake, ndiye kuti iwe ukukhala moyo. Mukuona? Iwe watsirizitsa kugula, zikatero, ndi kusinthanitsa, ndi zina zonse za izo. Izo zonse zakonzedwa. Inde.

<sup>272</sup> Anthu akugula, kuti akapeze kumene angakakhoze kukhala moyo wa mdziko mochuluka, Achipentekoste ndi onse. Kodi inu, Achipentekoste, si mumawaseleula a Baptisti ndi a Presbateria amenewo. Mphika sungaitche ketulo kuda. Ayi, bwana. Ayi, ndithudi. Zonsezo ndi zofanana. Kotero iwo akugula, kuti apeze kumene iwo angakhoze kupita mu tchalitchi ndi kukajowina bungwe, kuti iwo akhoze kukhala otchuka, oganiziridwa-bwino mu mzindawo, ameya a mzindawo amapita ku tchalitchi kumeneko. Chimene, iye akanakhoza kupita ku tchalitchi, ndi kukabadwa mwatsopano. Tsopano, ine ndikungonena, pakapita nthawi, mpingo wawukulu kwambiri mu mzindawo.

<sup>273</sup> Ine ndikuwadziwa anthu lero amene ali a bungwe laling'ono kumtunda kuno pa msewu, mpingo waung'ono, koma iwo unali waung'ono kwambiri. Kotero iwo anati, “Kotero athu—ana athu adzatero, ndipo ife tikhoza, kukhala oganiziridwako pang'ono,” iwo anatenga kalata yawo kuchokera ku mpingo umodzi ndipo anapita ku wina, bungwe lalikulu kwambiri. Ndipo pambali pake, winawu unali ndi chiwonetsero cha zithunzi mchipinda chapansi, ndipo iwo amakhoza kumasewera bunco ndi chirichonse monga choncho, inu mukudziwa, ndi kumakhala ndi masewero awa, ndi zina zotero monga zimenezo. Kotero iwo anawatengera ana awo kumeneko. Iwo anali ndi pool table mmusi kupansi, mwaona, kotero kuti iwo azikhoza kusewera pool, ndi kumakhala ndi zosangalatsa ndi zinthu monga zimenezo. Ndi kumakhala ndi kalasi ya Sande sukulu ya maminiti teni, ndi kupumulira kokamwa khofi, ndi kupumulira kuti abusa akakhoze kukasuta ndudu, kupita kunja. Oh, inde. Uko nkulondola. Ine sindikananena zimenezo pokhapokha ine nditadziwa zomwe ine ndikuzikamba. Uko nkulondola. Oh, ndithudi. Mukuona?

<sup>274</sup> Iwo akugula. Ngati iwo angathe kumapitirira ndi kumakhala moyo wa mtundu umene iwo akufuna kuti

aziwukhala, kumachita chirichonse chimene iwo akufuna, ndipo nkulonjezedwabe Moyo Wamuyaya pambuyo pake, iwo akugula kwa zimenezo.

<sup>275</sup> Ine ndikukuuzani inu, ngati inu mukufuna kuti mugule, bwerani ku Kalvare. Izo zimakhazikitsa zimenezo. Mufe ku zauve za inueni, machimo anu, ndipo mubadwe mwatsopano, katsopano.

<sup>276</sup> “Ndipo ngati inu mulikonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu nkomwe.” Izo ndi zimene Baibulo linanena. Uko nkulondola.

Mukuti, “Ine sindimakhulupirira mu chiyero.” Nzosadabwitsa, inu simungakwanitse.

<sup>277</sup> Koma Baibulo linati, “Popanda icho, palibe munthu ati adzamuwone Mulungu.” Mulungu ndi woyera. Ngati Mulungu akukhala mwa inu, ndinu woyera, nanunso.

<sup>278</sup> Ndipo mukundiuza ine kuti inu mungakhoze kumapita uko ku maphwando awa, ndi kukamwa chakumwa choledzeretsa pang’ono? Achipentekoste ambiri amachita zimenezo, amapita kunja ku maphwando awa, ndi kukawatengera akazi amenewo kunja uko ndi kumakakhala mmalo awa, ndi kumapita kumeneko ndi kumakadzivula nokha, ndi masuti osambira, ndi kumapita kumakasambira pamaso pa amuna, pamene amuna anu, ndi azichimwene, ndi azichemwali, ndi ena otero. Ndipo anthu Achipentekoste kumatuluka atavala masuti osambira, ndi kumadzitcha nokha membala wa Mkwatibwi? Mkwatibwi wa Khristu samachita zinthu zimenezo.

<sup>279</sup> Oh, iye akugula, ndithudi, akupeza njira yophweka, kenako nkulonjezedwa Moyo Wamuyaya pambuyo pake.

<sup>280</sup> Inu mulibe Iwo, pokhapokha ngati Iwo ukukhala mwa inu, Mawu a Mulungu kukhala mboni yamoyo kuti Iye ali moyo, ndipo inu mumakhala amoyo mwa Iye. Oh, mai! “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.” Oh! Osati tizikhulupiroro iti, osati zinthu izi zimene anthu amazipanga. “Ife tikufuna timuwone Yesu.”

<sup>281</sup> Koma Iye watayika, kwa iwo. Uh-huh! Bwanji? Mphindi yokha. Bwanji? Nchifukwa chiyani Iye watayika, kwa iwo? Nchifukwa chiyani Iye watayika, kwa a Pentekoste? Nchifukwa chiyani Iye watayika, kwa a Methodististi ndi a Baptististi? Nchifukwa chiyani Iye watayika, ku mabungwe amenewo? Chifukwa iwo samatenga njere yawo ya tirigu ndi kuyigwetsera iyo pansu pa Kalvare, ndi kufa ku kachikhulupiroro kawo, ndi kubadwa mwa Mawu.

<sup>282</sup> Ndiye ife timatsukidwa ndi madzi a Mawu, ameni, timadzakhala zolengedwa zatsopano mwa Khristu Yesu. Ndipo zizindikiro zimene Khristu anati zimamutsatira Iye, zidzawatsatira iwo. Mkazi aliyense adzabwera pa malo ake.

Mwamuna aliyense adzabwera pa malo ake. Mzimu wa Mulungu udzafika pa malo Ake, ndipo Mpingo wa Mulungu wamoyo udzakhala wopanda banga. Ndithudi. Amen. Inde, bwana. Umo ndi momwe izo zimachitidwira.

<sup>283</sup> Kulibe imfa ku njere yawo ya tirigu. Iwo samagwetsa chipembedzo chawo. Iwo samachilola icho kuti chife. Ngati bungwe la Baptisti likanagwetsera mbewu ya Baptisti ya tirigu ija mu nthaka ndi kuyisiya iyo kuti ife; ngati Amethodisti akanagwetsera njere yawo ya tirigu mkati, ngati a Assemblies of God, ndi a Pentecostal Jesus Name, ndi a Oneness, ndi Threeness, ndi onse osiyanasiyanawo, mpingo wa Mulungu, ndi ena onsewo, akanagwetsera njere ya tirigu ija mu Mawu; ndi kuilola iyo kuti ife ku malingaliro ake omwe, ndi kuwalola Mawu awa kuti akhale ndi kubwera ku Moyo. Ndiye iwo akanati, “Ngati inu simukundikhulupirira ine, mukhulupirire ntchito zimene ine ndikuzichita, pakuti izo ndi zomwe zikuchitira umboni za ine.”

<sup>284</sup> Ntchitozo ndi chiyani? Yesu anati, “Ntchito izi, ntchito zimene—zimene Mulungu anandipatsa Ine kuti ndizichite. Ndipo,” anati, “monga Atate anandituma Ine, chomwechonso Ine ndikukutumani inu.” Ntchito zomwezo zimene Mulungu ankazichita ali mwa Iye, zinamupanga Iye ndi Atate kukhala Mmodzi. Ndipo ntchito zomwezo zimene Yesu ankazichita, ndi Mzimu Woyera wa Yesu umene uli mwa inu, udzakupangani inu kuchita ntchito zomwezo. “Ntchito zimene Ine ndizichita iye adzazichita nayenso.” Ndithudi.

<sup>285</sup> Sanachilole chimangacho, hmm! Kodi iwo anachita chiyani? Mamembala akufa okha, akufa mu tchimo ndi zolakwa, akufa mu maphunziro, akufa mu zinthu za mdziko. Izo zimawerengedwa kwa iwo. Ndicho chifukwa chake iwo sali wobadwa mwatsopano, ndicho chifukwa chake zizindikiro sizikutsatira. Chifukwa chiyani? Mamembala akufa okha. Kuti akhale, mtumiki akuyenera kukhala ndi Ph.D, ma L.D. awiri, iye asanachite ubusa mipingo ina, ndipo mwinamwake iye samadziwa zilembo zoyambirira za alfabeti, ABC, “Nthawizonse Muzikhulupirira Khristu.” Ngati iye akanamukhulupirira Khristu. . .

<sup>286</sup> Mwamuna wina anandipanikiza ine, tsiku lina, ndipo anati, “Bwanji inu osawasiya anthu amenewo okha, nthawizonse mumawakhoma iwo za momwe iwo amavalira, zinthu zimene iwo amachita? Chabwino, ngati inu muli mneneri. . .” Iwo anati, “Anthu amaganiza kuti ndinu mneneri.”

<sup>287</sup> Ine ndinati, “Ine ndikudziwa kuti iwo akhala akunena zimenezo. Ine sindiri. Koma,” ine ndinati, “iwo—iwo—iwo ananena zimenezo.”

<sup>288</sup> Anati, “Chabwino, ngati iwo amakukhulupirirani kuti inu muli, ndiye bwanji inu osamawaphunzitsa iwo momwe

angamawonere masomphenya ndi kumayenda pamaso pa Mulungu?”

<sup>289</sup> Ine ndinati, “Ngati iwo sakumudziwa ABC, ine ndingawaphunzitse bwanji iwo algebra? Ngati iwo sakudziwa za sukulu ya mkaka, sadziwa momwe angakhalire ndi khalidwe, sakudziwa momwe angayang’anire ndi kuchita, ndi kuvala, ndi kukhala akhalidwe, iwe ungawaphunzitse bwanji iwo zinthu zauneneri?”

<sup>290</sup> Yesu anati, “Ngati inu simukukhulupirira zinthu za kuno, zinthu za padziko lapansi, inu mukhulupirira bwanji, Ine ndikakuuzani inu zinthu zakumwamba?” Zinthu zimene mungakhoze kuchita nokha, kusiya kuchita zinthu zimenezi. Mukulephera ngakhale kuti muchite zimenezo, inu mungapeze bwanji zinthu zauzimu, anthunu? Si kulondola uko? Inde, bwana.

Kufa kokha, ku maphunziro awo. Iwo ali ndi gulu lophunzira.

<sup>291</sup> Tsopano ine nditseka ponena ichi, mawu ochepa awa okha. Uthenga wanga wa Khristimasi, ndiwoti, ndiloleni ine ndikulozerani inu usikuuno ku mtanda. Amen. Ndipo inu, njere ya tirigu, mugwere mwa Khristu kumeneko ndipo mukafe. Kumeneko inu mukapeza Moyo Wake mu Mawu Ake, kukhala yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mulole umenewo ukhale Uthenga wanga wa Khristimasi kwa inu. Ine sindikukulozerani inu kodyera ziweto, ku chikuta, ku mpingo, ku chipembedzo. Koma, “mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu,” ndiye ine ndikulozerani inu kwa Iye. Iye akulozerani inu ku imfa Yake, kuyikidwa mmanda ndi chiukitsiro. Ndipo inu mulole mbewu yanu yomwe ya tirigu igwere mmenemo, ndipo mulole Mawu Ake akhale enieni mwa inu, ndipo inu mudzawona kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

Tiyeni tipemphere.

<sup>292</sup> Atate Akumwamba, ngakhale maorawa akusesa mopitirira, ndipo Mzimu Woyera ukuyenda pakati pa anthu, ndipo mawa likuyenera kukhala kupembedza kwa tsiku limene Inu munamutumiza Mwana Wanu wobadwa yekhayo mdziko. Ndipo ine ndayesetsa, usikuuno, kuti ndisawalozere anthu kodyera ziweto kumene Iye anabadwirako, pakuti Iye anali Khanda chabe nthawi imeneyo. Koma ine ndikuyesetsa kuti ndiwalozere iwo ku cholinga chimene Iye anabadwira, kuti Iye akhoze kukhala Mpulumutsi wawo, kuti Iye akhoze kukhala Mulungu wawo, yawo—yawo—yawo—Mfumu yawo, Zonse-mu-Zonse wawo. Kutu iwo akhoze kumudziwa Iye Amene amadzaza danga lonse, kuti iwo akhoze kumudziwa Iye; osati Mmodziyo yemwe anayambira ku Betelehemu, koma Mmodziyo

yemwe analibe konse chiyambi, Mmodziyo yemwe ali Mulungu Wamuyaya, yemwe ankakhoza kuyima pa dziko lapansi ndi kuti, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi.”

<sup>293</sup> Ndikuyesetsa kuti ndizichita ngati a—wophunzira, mopambana momwe ine ndikudziwira kuchitira. Pamene anthu a mtima wanjala anabwera kwa ophunzira amene anali owona, Filipo ndi Andreya, iwo anawatengera iwo mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, ndipo Iye anawalozero iwo ku imfa imene inali kudza, kuti iwo akhoze kumudziwa Iye ndi kumuwona Iye.

<sup>294</sup> Ndipo usikuuno, Atate, chimodzimodzinso, ine ndikuwalozero iwo ku Kalvare kumene Mwana wa Mulungu, Mulungu akuwonetseredwa mu thupi, anatenga mawonekedwe a munthu ndipo anali mkachisi, anasintha chigoba Chake, anakhala kuchokera ku... Mulungu Wamuyaya mu Ulemelero pamene Wamuyaya anadzakhala munthu ndipo anadzamanga hema Wake pakati pathu ndipo anadzakhala mmodzi wa ife kuti adzakhale Wowombola Wachibale, kuti atibwezeretsenso ife ku a—chiyanjano cha Mulungu wamphamvu amene anatilenga ife.

<sup>295</sup> Apo Iye anafa, pa Kalvare, ndipo apo ife tikuyenera kufa ndi Iye. Monga Iye anafera, Mwana wa Mulungu; kuti tikhale ana a Mulungu, ife tikuyenera kufa nafenso, ndi kulola njere yathu ya tirigu igwere mu nthaka ndi Iye, miyoyo yathu nkukhala yakufa ndi yobisika mwa Iye. Oh, ndipo kenako nkuwuka mu chiwukitsiro Chake, kuti tizipitiriza ntchito Yake, kuti tilole Mulungu Wake yemwe uja, yemwe anali mwa Iye, abweretse mawonetseredwe a Mawu a Mpingo mmasiku otsiriza ano, monga Iye analonjezera.

<sup>296</sup> Mulungu, ndife okondwa kwambiri kuwona kuti Iye watsimikizira chidutswa chirichonse cha izo, kuwonetsera kuti Iye ndi Mulungu. Iye amasunga Mawu Ake. Lawi la Moto lalikulu likadali pakati pathu. Zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zimene Iye anazilonjeza, zikuchitikabe.

<sup>297</sup> O Mulungu, ndife okondwa kwambiri kuti, usikuuno, kuti cholinga chimene chinamubweretsa Iye ku dziko lapansi, kuti ife tiri ndi ufulu wotengera Mzimu Wake mmoyoyo yathu. Izo zimatipatsa ife Moyo Wamuyaya, Mawu Ake kupangidwa thupi mu umunthu wathu womwe.

<sup>298</sup> Tiloleni ife tidzipereke tokha, usikuuno, Ambuye, tisiye kwathunthu, chirichonse cha mdziko lino, kuti ife tikhoze kufa ku zinthu za mdziko; ndi kuwuka kachiwiri ku Moyo watsopano mwa Khristu, kuti tilowe mu chaka chikubwerachi, ngati chakachi chingathe, kapena ngakhale icho chingafike pano. Ambuye Yesu, kuti tikhale atsopano, zotengera zopatulika za Mulungu, zotsukidwa ndi madzi a Mawu, kupyolera m’Magazi, ndi zoyikidwa pambali ku utumiki wa Khristu! Perekani izi, Ambuye. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu,  
 Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu;  
 Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

Tiyeni tikweze manja athu ndi mitima yathu, pamene ife tikuyimba iyo.

Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu,  
 Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu;  
 Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiyende ndi Inu.

<sup>299</sup> Tiyeni tiweramitse mitu yathu ndi mitima yathu, ndipo tiyimbe iyo mwakachetechete; koma kwa Iye tsopano, munga ngati inu mukuyang'ana molunjika kwa Iye.

Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu,  
 Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu;  
 Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

<sup>300</sup> Ngati umenewo uli umboni wanu, tsopano kwezani dzanja lanu. Nenani, “Pafupi ndi Inu! Zoonadi, Ambuye, osati mpingo, Inu! Osati kachikhulupiro, koma Inu. Osati kama kapena chikuta, Inu! O Mulungu, mulole Mawu Anu akhale mwa ine, kuti ine ndikhale pafupi ndi Inu.”

Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

<sup>301</sup> Tsopano pamene ife tikuyimbanso kachiwiri, gwirani, dzanja la winawake, munene, “Ine ndikupempherera iwe, Mkristu.” Pamene inu mukutenga dzanja lawo, ndiko kunena kuti, “Ine ndikupempherera iwe, Mkristu. Iwe undipempherere ine.”

Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu,  
 Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu;  
 Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

Tsopano pamene inu mwaweramitsa mitu yanu:

Modyera ziweto kalero, ndikudziwa kuti ziri  
 chomwecho ndithudi,  
 Mwana anabadwa kuti adzapulumutse anthu  
 ku tchimo lawo.  
 Yohane anamuwona Iye pa gombe,  
 Mwanawankhosa kwanthawizonse,  
 Oh, Khristu, Wopachikidwa wa Kalvare.

Pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu;  
 Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

<sup>302</sup> Inu mumamukonda Iye? Kodi Iye si wodabwitsa?

Wolumala anapangidwa kuti ayende,  
 wosayankhula anapangidwa kuti ayankhule,  
 Mphamvu imeneyo inayankhulidwa ndi  
 chikondi pa nyanja;  
 Wakhungu anapangidwa kuti apenye, ine  
 ndikudziwa zinachitika kokha  
 Chifundo cha Mwamuna waku Galileya uja.  
 Tsopano, pafupi ndi Inu, pafupi ndi Inu;  
 Paulendo wonse wamoyo,  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

<sup>303</sup> Icho ndi chokhumba chanu usikuuno? Nenani, “Ameni,”  
 ngati icho chiri. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Oh, ndi  
 zodabwitsa bwanji!

Pa ulendo wonse wamoyo, (Ndife  
 amwendamnjira.)  
 Mpulumutsi, ndiloleni ine ndiziyenda ndi Inu.

<sup>304</sup> Mulungu akudalitseni inu. Osati kwenikweni “Khrisimasi  
 yabwino,” koma madalitso a Mulungu a Khrisimasi akhale pa  
 inu. Mulole Khristu wa Kalvare akubiseni inu mwa Iyemwini,  
 akuphimbeni inu, akukulungeni inu ndi kukubisani inu mu  
 Mawu Ake, mpaka Mawu Ake asandulike thupi mwa inu, ndiro  
 pemphero langa. Mulungu akudalitseni inu. Abusa tsopano,  
 M'bale Neville. 

61-1224 Mabwana, Ife Tikufuna Timuwone Yesu  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)